

Ndi Chiyani Chokopa Pa Phiri?

Jeffersonville, Indiana USA

Julaye 25, 1965

1 Kungokhulupirira, kungokhulupirira,

Zinthu zonse nzotheka, kungokhulupirira.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano.

Atate mulungu, iro ndipemphero lathu lodzipereka usiku uno, kuwona zonse zimene inu mukuwachitira anthu mutsiku lino. Ndipo ife tikukupemphani inu, Ambuye, mulole ife tingokhulupirira, kungokhulupirira kuti icho ndi choonadi, Mawu olembedwa akuwonetseredwa kwa ife. Perekani zinthu izi, Atate.

Tsopano usiku uno ife tikufuna kuti tikuthokozeni inu chifukwa chakuwala kumene inu munakuponyera pa Malemba kwa ife m'mawa uno. Ndipo ife tikupemphera usiku uno, Ambuye, munzere uwo wapemphero, kuti inu mudzawatsimikizira Mawu Anu kukhala choonadi. Ife tikupempherera mipingo yonse ndi magulu amene asonkhana kozungulira zo - zo - zoyankhulira zazing'ono izo kunja uko kudutsa, kuchokera kufuko ili, njira yonse mpaka ku gombe lakumadzulo, kukwera mpaka kumapiri a Arizona, kutsika mpaka kuzigwa za Texas, njira yonse mpaka kugombe la kum'mawa, monse kudutsa ku dziko, Ambuye, kumene iwo asonkhana. Maora ambiri motalikana, ife tiri munthawi, koma, Ambuye, ife tiri limodzi usiku uno ngati chimango chimodzi, okhulupirira, tiyembekezera kudza kwa Mesiya. Ife tikupemphera, Atate akumwamba, kuti inu mumutumiza Iye posachedwa kwa Mpingo Wanu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

2 Inu mukhoza kukhala.

Moni wa chiKhristu kwa inu nonse amene muli pano usiku uno. Ine ndikupepesa kuti tikanali odzazana ndi othinana mpaka ife tikupuma moperewera. Ngakhale zobweretsa mpweya, nazonso zodzidziritisa mpweya, sizikuchita mokwanira, anthu achuluka kwambili. Ngati kukanangokhala basi kachisi ongodzaza anthu mwabwino, zobweretsa mpweya izo zikanakhoza kukuwumitsani inu. Koma tsopano aliyense ali ndi chokupizira, akudzakupiza, ndipo chobweretsa mpweya chikupemerera mwamphamvu monga icho chingathere.

Ife tikutumiza moni kuchokera ku Gombe la kum'mawa mpaka kumadzulo, kwa abwezi athu onse mwa Khristu, amene akumvetsera kuno. Ife tikutumiza moni uko ku San Jose, M'bale Borders, gulu lakumtunda uko. Ife tikutumiza moni kumtunda mu mapiri, Prescott, Arizona, kwa M'bale Leo Mercier ndi gulu lawo limene liri kumeneko kuyembekezera kudza kwa Ambuye. Ife tikutumiza moni kwa iwo amene ali mu Tucson, amene asonkhana usikuuno, akuyembekezera kudza kwa Ambuye. Mpaka mu Houston, Texas, kwaiwo amene akuyembekezera kudza kwa Ambuye. Uko mu Chicago, kwa iwo amene akuyembekezera kudza kwa Ambuye. Mpaka ku Gombe la kummawa, New York ndi Connecticut, ndi magulu akulu kumtunda uko, amene akuyembekezera kudza kwa Ambuye. Ife tiribe malo pano oti tiwakhazike iwo, chotero ife tingowatumizira iwo Mawu kupyolera mu - njira ya lanya. Ife tikutumiza moni kwa M'bale Junior Jackson usiku uno, ndi gulu lake uko mu Clarksville. M'bale Ruddell, apo pa 62, ndi gulu lake, akuyembekezera kudza kwa Ambuye. Ndiye ife tasonkhana pano usiku uno ku mpingo wakwathu, kachisi, tikuyembekezera kudza kwa Ambuye.

3 Ndipo tsopano, ochuluka ainu mwina panalibe pa utumiki m'mawa uja. Koma ine ndikudalira kuti aliyense, amene panalibe, akatenga tepi imeneyo, pakuti ine ndikukhulupirira kuti iwo unali Uthenga olunjika kwambiri kwa mpingo kuchokera pa - Uthenga wa mabwana, ndi nthawi yanji ino? Ine ndinamverera kudzoza kwa Mzimu, ndinamverera kutsogozedwa kuti ndinene chimene ine ndinanena. Izo zinali motalika, komabe ine ndinamverera kutsogozedwa kuti ndichite izo. Ndipo ine ndikuganiza Ambuye, mwa Mawu Ake, anasonyeza ora lomwe ife tiri kukhalamo. Ndikutsimikiza kuti ife tikumvetsa zinthu zachinsisi izi zomwe zikuchitika. Inu mukudziwa, Baibulo linati, "Anzeru adzamvetsa."

Koma fuko ndi anthu adzapitirira "mukufooka ndi mwanzeru." Tangolingalirani, achiMerica apakati tsopano ali mu usinkhu wapakati, akakhala a pafupi zaka makumi awiri, ofookera koma anzerupo. Iwo sanalinazo ndege za Jeti mu masiku amenewo, ndi - ndi mizinga ya atomiki, koma iwo ankakhala moyo motalika kwambiri. Ife tikukhala ofookera ndi anzerupo, ndipo nzeru zathu zomwe ndi zomwe ziti zidzatiwononge ife. Ife tidzatiwononga tokha. Mulungu sadzatiwononga ife; nzeru zathu zidzatiwononga ife. Izo nthawi zonse zakhala mwanjira imeneyo. Ndipo chomwecho izo zidzakhalanso.

4 Tsopano, Ambuye akalola, la Mulungu lotsatira m'mawa, posadziwa tsopano pa chimene ine nditi ndidzayankhule, koma ine ndikudalira kuti Ambuye, ngati iwo atilora ife kuti tikhale moyo ndipo pakapanda kukhala chochitika, ndipo icho chikhala chifuniro chake, ife tikulinga kuti tiyankhule Uthenga wina la Mulungu lotsatira m'mawa, tidzakhala ndi kupempherera odwala la Mulungu lotsatira usiku. Ndiye maere agwera pa ine kuti ndibwerere kwathu ku Arizona, kuti ndi bwerere nalo banja kuti ana akakhoze kulembetsa musukulu. Ndiye inu mudzakhala... Ife tidzakudziwitsani inu, monga ife tingathere, zamisonkhano pamene iyo ifika, kapena nthawi zimene ife... Malo amene ife tikulinga kuti ife tikakhaleko. Chotero, Mulungu akudalitseni inu nonse.

Tsopano usiku uno, podziwa kuti ndi... Ine ndachedwa ndi mphindi khumi ndi zisanu, kuti ndiyambe, mphindi khumi ndi zisanu isanakwane 8 koloko kuno ku Jeffersonville; ndipo ndiyo pafupi mphindi khumi ndizisanu isanakwane 9 koloko ku Gombe laku m'mawa, ndiyeno ilipafupi 5 koloko ku Gombe la kumadzulo. Chotero tsopano ife tangotsala pang'ono kuti dzuwa lilowe kuno. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyankhule ndi inu kwa nsonkhano wa nthawi yochepa basi, kuti ndiyesere kupeza kudzoza kwa Mzimu, ndiyeno nkuyitana mzere wa pemphero.

5 Ndipo ine ndikufuna osonkhana pano, monganso osonkhana amene asonkhana kumalo ena, mupeze munthu wina, m'bale wina yemwe ali odzozedwa ndi Mzimu; ndipo pamene ife tiyamba kupempherera odwala, apite akuyika manja pa iwo amene ali mu osonkhana anu. Kumbukirani, Mulungu ndi opezeka ponseponse; Iye ali kulikonse. Chotero, kumusi mu Texas, mpaka mu California, uko mu Arizona, kulikonse kumene inu muli, ikani manja kwa iwo omwe akudwala pamene ife tidziyamba kupempherera odwala. Ndipo ine ndiri wotsimikiza Mulungu amva ndikuyankha pemphero.

Chinthu cha chodabwitsa, usiku wa Mulungu lapitalo, ndipo kudzoza kunali kukupitirira, ndipo Mzimu Woyera... Icho chinali chinthu ndithu. Ine ndakhala ndiribe - mzere wakuzindikira za mumtima kwa miyezi ndi miyezi, chikhalireni ndirikuno nthawi ina ija. Ndiyeno kuti upite apo pansi pa lonjezo... Iwe sukudziwa kuti Iye azichita izo. Iwe sungakhoze kunena kuti Iye azichita izo. Iwe umangoyenera kuti upite apo ndikukayembekezera. Iye ndiwochita mwayekha. Iye amachita zimene Iye akuzifuna. Koma kukaima pamene ndikudikira kuti uwone chimene Iye ati achite, ndiye nkumamverera izo zikufalikira pa iwe monga choncho.

6 Ndipo pamapeto pa msonkhano, posadziwa yemwe uyo anali, koma kunali - mwamuna penapake motsatira mzere uwo yemwe anali wamtali, ndi dazi pamwamba, ndipo iye anali munthu wodwala kwambiri.

Ndiyeno pamapeto pomwe, panali mwamuna anawonekera kuno pansanja, ndipo iye anali ataweramitsa mutu wakeake, ndipo iye amawoneka ngati anali kuvutika, atadzigwira yekha chapamimba. Ndipo ine ndinaganiza kuti uyo ayenera kuti anali munthu oyamba uja kapena munthu wachiwiri, kapena paliponse pamene panali pamene ine ndinamupempherera iye, chifukwa iye anali wadazi ndipo anali ataweramitsa mutu wake pansi; munthu wamkulu, atawerama. Koma ine ndinayang'ana pozungulira ndipo ine ndinapeza njondayo itakhala panja apo, koma iye anali akusangalala. Ine ndinaganiza, "Izo ziri kuti?" Ine sindikanakhoza kulingalira pamene izo zinali. Ine ndinakhoza kuzimverera izo ndikumuna bamboyo patsogolo panga.

Ine ndinamverera izo zikukokera chakumbali iyi, ndipo izo zinali zikubwera kuchokera kumbuyo. Ine ndiyang'ana pa M'bale Neville ndi awiri awa atakhala apa, izo sanali iwo. Ine ndinati, "Bamboyo ali nkati mobatizira umo kumbuyo uko." Ndipo inu mukudziwa yemwe iye anali? M'bale Shepherd. Chifukwa chimene ine sindimakhoza kumuzindikira iye, iye anali atakhala kumbuyo uko ali ndi mutu wake utaweramitsidwa, akupemphera.

Iye amaganiza kuti akanati afe, amalingalira izo kwa masabata pang'ono apitawo. Mkazi wake anamuza iye kuti apite akagule nsapato za tsopano, ndipo iye anati, "Ine sindizisowa izo. Ine sindikhala kuno motalika chotero."

7 Ndipo iye anakumana nane tsiku lina mu ... kumtunda uko pabwalo, la M'bale Wood, akufuula ndi kutamanda Mulungu. Anati, "Ine ndikudya nyama ya nkhumba, mazira, tomato, chirichonse chomwe ine ndikuchifuna."

Ndipo modzichepetsa kusiya mpando wake, kupita m'mbuyo nkati umo kuchoka panjira, ndi kumapemphera. Mukuona, inu simumasowa khadi lapemphero, inu mumangosoweka chikulupiri. Mukuona. Tsopano, ine sindinadziwe ngati iye anachiritsidwa kapena ayi, ine ndingoti, "Mu - bamboyo, akupemphera, iye ali ndi chinachake cholakwika." Ine ndikuganiza iwo unatchula chimene icho chinali, "vuto la mmimba, ndipo anapemphera m'mbuyo kuseri kuno. Ambuye Yesu akupangeni inu wabwino." Tsopano, ndizo zonse zimene ine ndikanakhoza kunena. Kukokako kunali kuti iye anali akupemphera. Ine ndimakhoza kuziona izo, koma zimene zingachitike ine sindikudziwa, Mukuona.

Koma pamene iwe umva Iwo ukubwerera, aliyense akuzindikira, pameme Iwo uti, "PAKUTI ATERO AMBUYE," mwaona, izo si ine ndikuyankhula aponso ndi Iye; uyo ndi Iye.

8 Koma ine nthawi zonse ndimati, "Yesu Khristu wakupangani inu wa ngwiro," icho ndi ndendende Choonadi. "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa." Mukuona, Mukuona.

Koma pamene izo zibwera, "PAKUTI ATERO AMBUYE," ndikukuuzani inu choti muchite ndi chimene chiti chichitike, penyani izo, izo zikhala mwanjira imeneyo.

Koma pamene ine nditi, "Yesu Khristu wakuchizani inu ndipo wakupangani inu wangwiro," inu mukhulupirire izo, chifukwa Iye ananena kale izo. Ine ndikungobwereza zimene Iye ananena.

Ndipo masomphenya ndikungobwereza zimene Iye anawonetsa. Inu mukumvetsa?

9 Tsopano tiyeni ife tifulumire ndikulowa kumene mu Mawu, chifukwa ine ndikudziwa kuti ambiri a inu mulipano, muli ndi ma mailosi aatali kuti muyende usiku uno. Ine ndikupemphera kuti Mulungu akudalitseni inu, akuthandizeni inu ndikukutetezana inu pamisewu. Ndipo tsopano ine ndikukhumba kuti nditembenuzire usiku uno ku Mateyu Woyera, mutu wa 21, ndi ndime 1 mpaka 11, mu Mateyu Woyera. Ndipo, tsopano, ngati inu mulibe Baibulo lanu, kapena ngati inu mukufuna kuti mudzilemba Malemba awa, chabwino.

10 Ndipo tsopano kwa inu amene simunaumve konse Uthenga m'mawa uja, ndipo inu muli ndi tepi rekoda; ife sitimalimbikitsa, kugulitsa matepi. Ife sitimalimbikitsa, kugulitsa chiri chonse. Nthawi zina mu nsonkhano wawukulu iwo amalengeza kuti iwo ali ndi mabuku ena kumbuyo uko; ife sitimapeza kalikonse kuchokera kwa iwo. M'bale Vayle ndi mulembi. Matepi, bambo yemwe amachita malonda amatepi uko angakuwuzeni inu, ife sitipeza ndalama za matepi. Ife siti... Si "matepiwo;" ndi Uthengawo. Ndipo pamene munthu ayika mumalingaliro ake kuti ndindalama, iye sapanga matepi mopitiriranso. Ndiko kulondola. Ine ndinali kufunsa zaizo, ine ndikuganiza matepi athu amagulitsidwa pafupi, pansu pa madola asanu, kapena china chake, atatu mpaka asanu, kapena china chake monga choncho. Mwati chiyani? Atatu ndi anayi, kwa matepi aakulu, aatali awo.

Ndipo mulaliki wina ine ndinamufunsa za imodzi za matepi ake, ndipo iyo inali madola asanu ndi anayi, pafupi mphindi makumi awiri kapena atatu, authenga.

11 Chotero ine ndikuona kuti M'bale wathu Sothmann kumbuyo uko sakuyamba kulemera, aliyense waiwo, pamatepi awa amene iwo ali - iwo akuwapanga. Mwaona, iwo amangopanga zokwanira kuti adzipitirira nazo pa izo. Sungakhoze kuwafunsa iwo kuti adziwapanga iwo mwa ulere, chifukwa iwo amachita kugula matepi ndichinthu chiri chonse. Ndipo makina ndi odula kwambiri, amagulitsidwa pafupi madola zikwi khumi kuti akhazikitse kuti azipanga matepi amenewo, pakuyamba nazo.

Tsopano, ine ndamva posachedwapa ine... Sindinalengeze izo panobe. Koma pakhala kumvetsera kwa tepi naponso. Nthawi zowirikiza chotero ife... Matrasitii, ine ndiribe kanthu kochita ndi izo komwe. Ine ndiribe ngakhale... Osati pa uliwonse wa misonkhano. Ndizo mwina - sindizo zovomerezeka kapena zosavomerezeka. Iwo amapereka mitengo yawo; matrasitii amalingalira yemwe ati akhale munthu otsatira kuti adzipanga matepi, ndipo iwo amamutumizira iye kalata. Ndizo zonse zimene ine ndikuzidziwa za izo. Iwo amasamalira za izo, chifukwa ine sindingakhoze ngakhale kudalitsa ana ndiye ati kusamalira matepi, chotero... kapena kubatiza.

12 Chotero ine malingaliro anga ndawaika pa Uthenga uwu, ndicho chikoka chachitatu chija, ndipo ndichomwe ine ndiyenera kukhala kumvera ndi wolemekeza kwa icho.

Mateyu 21:1 mpaka 11. Ine ndinanena izo kuti inu mukhoze kukhala mukuyembekezera... Kapena kutembenezira ku Malemba

Ndipo pamene... Ndipo pamene iwo anayandikira ku Yerusalemu, ndipo anafika ku Betefage, ku Phiri la Azitona,... Yesu anatumiza awiri awophunzira ake

Ndikunena kwaiwo, mukani kumudzi openyana ndi inu uwo, ndipo molunjika inu mukapeza buru omangidwa, ndi mwana wamwamuna ali ndi iye: mukawamsule iwo, ndipo muwabweretse iwo kwa ine.

Ndipo ngati munthu wina akanena kanthu kwa inu, inu mukati, Ambuye akudzisowa izo; ndipo pomwepo iye akawatumiza iwo.

Izi zonse zinachitidwa, kuti chikakwaniritsidwe chimene chinanenedwa ndi mneneri, kuti,

Awuzeni inu ana akazi a Zioni, taonani, mfumu yanu ikudza kwa inu, ofatsa,... Atakhala pa buru, ndi pa mwana wa phongo wa buru.

Ndipo ophunzira anamuka, ndipo anakachita monga Yesu anawalamulira iwo,

Ndipo iwo anabweretsa buru, mwana wa mphongo wake, ndipo anayika paiwo zovala zawo, ndipo anamukhazika iye pamene.

Ndipo unyinjira waukulu kwambiri unayala zovala zawo munjira; ndipo ena anadula nthambi za mitengo ndipo anaziyalala izo munjiramo.

Ndipo unyinjira unapita patsogolo, ndiumene unkatsatira, unafuula, kuti, Hossana kwa mwana wa Davide; wodala ali iye amene akudza mudzina la Ambuye; Hossana m'mwambamwamba.

Ndipo pamene iye anadzalowa mu Yerusalemu, mzinda wonse unagwedezeka, nanena, ndindani uyu?

Ndipo unyinjira unati, uyu ndi Yesu mneneri waku Nazaterete wa Galileya

Tsopano ngati ine nditati nditenge mutu kuchokera pamene, kwa pafupi mphindi makumi atatu

mzere wa pemphero usanayambe, ine ndikanafuna kuti nditenge uwu ngati mutu: Ndi Chiyani Chokopa Pa Phiri?

13 Tsopano, ilo linali tsiku lotopetsa kwambiri, lonjenjemeretsa, ndipo ilo linali tsiku losazolowereka. Ife tikumupeza Yesu apa akubwera ku Yerusalemu, okonzeka kuti akakhale nawo pa pasakha. Ndipo pasakha ndipamene mwana wankhosa wa pasakha anali kukaphedwa, ndipo magazi anali kuwazidwa pa mpando wa chifundo mwa - mwachitetezero kwa - kwa anthu. Ndipo Iye anali atabwera kuchokera ku Betefage ndipo anali atabwera mpaka pa mwamba pa phiri la Azitona limene limayang'anira pansi pa phiri lina laling'ono pamene Yerusalemu anamangidwapo. Ndipo pamene Iye ankayang'ana, ndipo ankadziwa kuti uku kunali kudzachezako Kwake kotsiriza.

Iyi inali nthawi yomwe Iye akanati aperekedwe m'manja a anthu ochimwitsitsa ndipo iwo akanamupha Iye. Iye akanafa imfa yoopsetsetsa imene inayamba yafedwapo ndi munthu wa thupi lakufa aliyense, ndikukaikidwa m'manda. Iye akanati aperekedwe ndi Ake womwe, ena aiwo atayima pomwepo ndi Iye. Ndipo Iye, kukhala Mulungu ankadziwa chimene chinali mu mitima yawo ndipo ankadziwa kuchokera pachiyambi yemwe akanati adzamupereke Iye. Ndipo ankadziwa munthu ameneyo anali ndi Iye yemwe ankakhala pambali Yake ndipo ankawerengera ndalama Zake kwa Iye, ndi zina zotero, ankadziwa kuti munthu ameneyo akanati adzamupereke Iye. Ndipo ankadziwa kuti mtanda wankhanza wa chi Roma unkamuyembekezera Iye kumeneko. Iye ankadziwa kuti madzi ake muthupi Lake ndi magazi ake muthupi Lake zikanati zilekane, ndikuti magazi akanati agwe kuchokera pamphumi Pake, madontho akulu onga thukuta. Iye ankadziwa kuti zonse izo zinali patsogolo Pake. Ndipo Iye akuima pa Phiri, kuyang'ana chaku Yerusalemu.

14 Anthu a tsiku limenero, a... chimene iwo ankachitcha tsiku limenero, "gulu labwinoko la chipembedzo," linkamuda Iye. Mipingo ya tsiku limenelo inkamuda Iye ndipo inkamunyoza Iye, ndipo ankawanyoza onse amene ankamumvetsera Iye. Ndipo ngati iwo anapita nakakhala nawo pamisonkhano Yake, iwo mwansanga anali kuchotsedwa pachiyanjano champingo. Palibe zodabwitsa Lemba linati, "Iye anadza kwa ake omwe, ndipo ake omwe sanamulandire Iye." Iwo amene akanayenera kuti adzimukonda Iye, iwo amene akanayenera kukhala a Iye, anali adani Ake, mowawitsa.

15 Ndipo Iye anali atapanga gulu Lake laling'ono kuchokera ku mulu wa anthu osawuka, asodzi, osonkhanitsa misonkho, osaphunzira. Baibulo linati ena aiwo anali ngakhale "mbuli, osaphunzira." Ena sankakhoza ngakhale kulemba dzina lawo. Iye sanapite konse kwa mipingo kuti akatengeko anthu ake ake.

Ndipo Iye sanali kugwirizana konse ndi aliyense wa atsogoleri amipingo. Ndipo, pambali pa izo, Iye ankatsatira kachitidwe konse ka mneneri. Iye ankatsutsa chiri chonse chimene iwo ankachichita monga iwo apambuyo Pake ankachitira; chifukwa iwo anali ka gawo ka Mawu, ndipo Iye anali Mawu muchidzalo chake.

16 Koma nkati mwa izo zonse, kupyola mubadwo uli wonse ndi mneneri aliyense yemwe anakhalapo kapena akanadzakhalapo payenera kukhala kuchuluka kwina kwa anthu amene ali okonzedweratu kuti adzamve Uthenga umenewo, ndipo iwo akanadzautsata iwo. Amenewo sakusamala maunyanji. Iwo sankasamala kutsutsa kwa wosakhulupirira. Iwo alibe chotsutsa ndi iwo. Iwo alinacho chinthu chimodzi choti adzichita, ndicho kukhulupirira ndikuti atenge chidutswa chiri chonse chimene iwo angathe, kuchinyika icho mkati mwawo monga Maria yemwe ankakhala pa mapazi a Yesu.

Ndipo Malita anali kukonza chakudya Chake, ndipo Yesu ananena kwa iye, "Koma Malita, iwe uli okhudzidwa kwambili ndi zinthu za moyo koma Maria wafuna zinthu za bwinoko," mwaona, zinthu za Moyo wa muyaya.

17 Tsopano, ife tikupeza kuti ochuluka a anthu amene anali atamvetsa... Iwo analibe zowerenga monga ife tiri nazo lero, iwo analibe wailesi yakanema kapena malamya, kapena chiri chonse chatsiku limenelo, koma amakhala ngati alandira mphekesera yakuti Iye adzakhala nawo pa pasakha. Pakuti ochuluka aanthu, pokhala amalingaliro - a uzimu, ankadziwa kuti Iye anali Mwana wankhosa wa pasakha uja chifukwa Iye anali atawauza kale iwo zinthu zomwe zinkati zikachitike.

18 Ndiye, ndithudi, podziwa kuti Iye anali oti adzakhalepo kumeneko, ndipo ankamukonda iye momwe ankamukondera, iwo anali kumuyembekezera Iye. Uko kunali unyanji umene mwina unali ukukankhana, kuponyana kuchokera kuchipata chimodzi mpaka kuchinzake, kuyang'anira kumbali iriyonse, pakuti iwo ankadziwa kuti limodzi la ma ora Iye akanati awonekere. Iwo anali akuyembekezera.

Ena anali akudabwa chimene chinali vuto ndi anthu awa akuthamanga kuchokera kuchipata mpaka kuchipata. "Ndichiyani chokopa?"

Ndipo iwo amakhoza kuyang'ana mbali iyi ndikuyang'ana mbali iyo, kuti apeze. Zinkawoneka ngati kuti iwo anali kufunafuna china chake, pansi pachiyembekezo cha china chake choti chichitike.

O, momwe ine ndikanafunira kuti ndisinthe mutu wanga kwa mphindi zochepe ndikunena ichi, kuti

ndichomwe lili vuto lero. Anthu amene akumuyang'anira Iye pakudza ali pansa pa kuyembekezera kwakukulu ndi chiyembekezero. Iye tikukhoza kumverera izo, chiposyinjoko. Ndipo iwo akufunafuna, kuyang'ana kusuntha kulikonse ndi chizindikilo chiri chonse, kufanizitsa icho ndi Malemba.

19 Ndipo pamene iwo anali atawona zinthu zonsezo zimene zinaneneredweratu za Iye, mpaka pa mapeto pomwe, iwo ankadziwa kuti mapeto anali atayandikira. Iwo ankafuna akakhale kumeneko, chotero iwo anayang'anira. Gawo la unyinjoko lina la kwa Iye, mwa kuchepa. Ena anali omutsutsa Iye, ochuluka aiwo magawo makumi asanu ndi anai pazana anali omutsutsa Iye.

Ndipo ndizo pafupi momwe izo ziliri lero mu unyinjoko wazipembedzo, pamene izo zifika penipeni pa Mawu ndi Khristu, pamakhala pafupi m'modzi pazana amene angati akhulupirire izo. Gawo linalo sirimapereka chidwi kwa izo, ziribe kanthu zimene zikanachitidwa, iwo akhoza kumanena mtundu wina wanthabwala kapena kuponyera kachipongwe ka izo. Mpafupi mofanana basi. Nthawi, zinthu sizimasintha mochuluka kwambiri, mbiri yakale imangozibwereza yokha mozungulira.

20 Chabwino, ife tikupeza kuti izo zinabweretsa chikhalidwe chamanjenje. Izo zinkayenera kutero. Izo ziyenera kuchita izo. Iwo anali akudikira, iwo anali kulingalira chimene Iye akanati akachite pamene Iye akanafika kumeneko. Iwo ankafuna kuti akakhale kumeneko kuti akamve chiri chonse chimene Iye ati achite. Iwo ankazifuna izo. Iwo ankafuna kuti aziwone izo. Iwo ankamukhulupirira iye. Ena anali atamva kuti Iye anali kubwera, ndipo iwo anapita kumtunda uko kuti akamunyoze Iye. Chotero kutatha kuyembekezera konse kwa manjenje, tsiku losazolowereka kwambiri, nthawi yosazolowereka, mipingo itagona, mitsempha ya anthu inali pamalire, kunali anthu ochuluka kwambiri kumeneko, ndiyeno izo zinachitika.

21 Pa mwamba pa phiri la Azitona panabwera buru wang'ono, woyera akubwera, akuyenda chotsika phiri, ali ndi gulu la anthu akufuula motentheka, akukhadzula makhwatha akanjedza kuchokera ku mitengo, akuponyera zovala zawo munsewu, kufuula, "Hossana kwa mwana wa Davide amene akubwera mu Dzina la Ambuye!" Buru wang'ono uyu, onkwera wake sanali wina kuposa Mesiya odzozedwa wa Mulungu wa oralo.

Mulungu, ndiye, kodi Iye anali akuchita chiyani? Ndichiyani chokopa pamwamba pa phiri paja? Ndi Mulungu akupanga mbiri yakale, ndi Mulungu akukwaniritsa uneneri. Ndipo izo nthawi zonse zimayambitsa chokopa. Izo zimabweretsa otsutsa onse apo, miyimba (ya Uthenga wa m'mawa uja), ndi mphungu nazonso. Mukuona? Izo zimabwera palimodzi kuti zidzapeze chimene chiri kuchitika. Ena amabwera chifukwa cha chidwi, ena amabwera kuti apeze cholakwika, ena amabwera kuti adzatsutse. Pamakhala pali mitundu yonse itasonkhana, monga ife tinanena m'mawa uja: okhulupirira, odzipangitsa - kukhulupirira, ndi osakhulupirira. Ndi chiyani chiri pa phiri? Uneneri uli kukwaniritsidwa. Tsopano ife tiona zimene ziti zichitike.

22 Tsopano, mu buku la Zakaliya, mu mutu wa 9 ndi ndime ya 9. Zakariya, m'modzi wa aneneri, anayankhula mwa Mzimu kunena izi.

Sangalalani kwakukulu, O, ana akazi a Zioni; fuulani, O, ana akazi a Yerusalemu: tawonani, mfumu yanu ikudza kwa inu: iye ali olungama,... Alinacho chipulumutso; ozichepetsa, ndipo atakwera pa buru, wang'ono, mwana wa mphongo wa buru.

Tsopano, kodi vuto linali chiyani ndi alembi amenewo? Vuto linali chiyani ndi ansembe amenewo? Vuto linali chiyani ndi anthu achipembedzo amenewo? Izi zinalembedwa zaka mazana anayi makumi asanu ndi atatu ndi zisanu ndi ziwiri izo zisanachitike, ndi uneneri wotsimikiziridwa, ndipo zinali zitayikidwa kale mwa zolemba ndipo zinkatchedwa Baibulo, mipukutu ya chipangano chakale. Nchifukwa chiyani iwo sankakhoza kuwona kuti uwo ndi uneneri ukukwaniritsidwa? Ndi chifukwa chomwecho chimene iwo sangakhoze kuziona lero. Iwo anali atatenga Mawu a Mulungu ndipo anawapanga iwo kukhala opanda - mphamvu kwa anthu, pakuphunzitsa (mwa miyambo) mwa chiphunzitsa miyambo ya anthu.

Ndipo ngati mulembi, alaliki, atumiki, anthu auzimu (otchedwa - choncho), odzozedwawo, akanawerenga kokha Baibulo, iwo sibwezi akudabwa chimene chinali kuchitika, iwo bwezi atadziwa chimene icho chiri. Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake.

23 Mbiri yakale inali ikupangidwa, uneneri unali ukukwaniritsidwa. Chipulumutso kwa dziko chinali chikufika, tsiku lalikulu limene aneneri onse anali akuliyang'anira. Onse amene anali m'manda anali kuyembekezera tsiku limeneli (Taganizirani za izo), onse amene anali atafa, kulungama konse kwa magazi aofera ndi aneneri.

Zimene, Iye anali atangozifuula, "Yerusalemu, O, Yerusalemu, iwe amene umagenda mneneri aliyense yemwe Ine ndimutumiza kwa iwe, ndi kupha olungama, ndimowilikiza bwanji ine ndingakufungatire iwe monga nkukhu ichitira, ingachitire anapiye ake koma iwe sungatero ayi. Koma tsopano ora lako lafika."

24 Chiri chonse chimene chinali m'manda, Abrahamu, Isaki, Yakobo, aneneri onse, anali akuyembekezera ora iri.

Ndipo mpingo unali wa khungu kwa izo. "Uyu ndi ndani akuyambitsa phokoso lonseli? Ndindani nyamata ameneyu?" Iwo ananena nthawi ina, "Kodi ameneyo simwana wa akalipentala kuno? Ife tikumudziwa Iye. Kodi nzeru izi Iye anakazitengera kuti? Bwanji, ife sitikumona Iye atalumikizana ndi iriyonse ya masukulu athu. Ife sitikudziwa mabuku aliwonse omwe Iye anayamba waphunzira kuchokeramo. Ndindani Iye?"

Iye anali yankho la uneneri wa mneneri. Apa Iye akubwera, atakwera pamwana wa buru. Ndichokopa bwanji! Mulungu anali akukwaniritsa Mawu ake olonjzedwa, ora limene anakhala akulidikirira kuchokera zaka zikwi zinai. Mu Genesesi, mutu wa 3 ndi ndime ya 15, Mulungu anali ataneneratu, "Mbewu ya mkazi idzavulaza mutu wa serpent, koma mutu wake udzavulaza chidendene chake," uneneri umenewo kupyola mu Baibulo monse umene unanenedweratu za munthu uyu akubwera.

25 Ndipo kuno posakhalitsa pomwepa kunali mneneri anali ataimirira pakati pa iwo, amene anali mneneri wotsimikiziridwa, Zakaliya, ndipo Iye ananena, kuti, "Inu ana akazi a Yerusalemu ndi inu ana akazi a Zioni, sangalalani, fuulani, kuwani mokweza, pakuti mfumu yanu ikudza kwa inu, ofatsa ndi otsika ndi odzichepetsa, atakwera pamwana wa buru."

Ndipo pano anthu awo amene ankawerenga Lemba, tsiku ndi tsiku, anamuyang'ana Iye akubwera atakwera, ndipo anafuula, "Ndindani ameneyo?" Mwawona? Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake kwa anthu amene akanayenera kudziwa chimene icho chinali, koma iwo sanadziwe icho.

Pamene Mulungu akwaniritsa Mawu ake, icho nthawi zonse chimayambitsa kukopa nthawi zonse zimatero. Zimayambitsa kukopa, pakuti icho ndi chosazolowereka. Chosazolowereka kwambiri, pamene Iye akukwaniritsa Mawu ake kwa kachitidwe kamakono kwa tsikulo, chifukwa kachitidwe kamakono ka tsiku sikamakulupirira mu izo. Iwo ali nayo njira yawo yawo.

26 Tsopano, ife tikuona.. Ndipo tiyeni ife tibwerere mu Malemba ndipo titenge kuchokera muzochitika zina zosazolowereka, kwa mphindi pang'ono ena okha, pamene Mulungu anakwaniritsa uneneri wake. Pamene Mulungu anena chiri chonse, Iye achichita icho. Miyamba yonse ndi dziko lapansi zonse zidzachoka, koma Mawu amenewo sangakhoze kuchoka. Chotero iwo kawirikawiri amayambitsa chooneka, chooneka chosazolowereka.

Zindikirani kupusa kwake momwe Mawu a Mulungu aliri kwa - anthu amene amayenera kuti awakhulupirire iwo, ndipo izo ndizosazolowereka kwambiri ndipo iwo amafuula, "Chabwino, ichi ndi chiyani? Kodi iwe unazitenga kuti zinthu zimenezo? Ndindani ameneyu? Ndichiyani ichi?"

Pamene, iwo amayenera kuti adzifuula, "Hossana kwa mfumu amene akudza mu Dzina la Ambuye!" koma uko kunali kagulu kakang'ono kokha kakuchita izo, kagulu kakang'ono kokha. Zaka zwiwizi zinayi za uneneri, wachinthu chachikulu kwambiri chimene chinayamba chachitika kwa fuko, pakuti chiyembekezo chonse cha a kufa chinagona paicho, tsogolo lonse linagona mu icho; ndipo anthu achipembedzo, amene amazinenera kuti amakhulupirira icho anali kufuula, "Ndindani uyu? Ndipo nchiyani chokopa ichi?" China chake chosazolowereka! Pafupi zofanana, izo sizikusintha basi, tsopano zosazolowereka.

27 Tiyeni tiwone zina za zinthu zosazoloweka, monga ine ndangonena. Chinali chiyani chokopa chiweruzo chisanakanthe pamene dziko ndikuliwononga ilo ndi madzi? Munthu wachikulire, wapafupi usinkhu wazaka zana ndi makumi awiri, akumanga ngalawa pamene kunalibe madzi woti ayandamitsepilo. Kumtunda uko kwa zaka, ataima pakhomo, akumanga pamene, m'katimo, ndikulimata ilo mkati ndikunja, ndikumati, "Dziko lidzamezedwa ndi madzi," mum'badwo waukulu wa sayansi.

"Ndi chiyani icho chikugogoda uko pa Phiri pa mwamba apo?" "Bwanji, ndi bambo wachikulire dzina lake Nowa ndipo iye ali pamwamba apo, otentheka wachikulire. Bambo wachikulireyo wayima mudzuwa motalika kwambiri. Iye wakanthidwa ndi dzuwa. Iye wasokonezeka malingaliro ake. Ndipo iye akumanga chimene iye akuchitcha 'chombo,' ndikumati madzi akubwera kuchokera kumwamba uko kumene kulibe madzi, ndipo icho chidzayandamitsa anthu onse kumeneko; ndipo aliyense amene sati amvere Uthenga wake, ndi aliyense amene sati adzalowe mu chombo chimenecho, akuti adzamizidwa. Kodi inu munayamba mwamva za chinthu ngati chimenecho?" Icho chinali chokopa chosazolowereka.

28 Ine ndikulingalira pamene anthu afuna kuseka kwa bwino, iwo ankapita uko ndikukaima pafupi ndi chitseko cha chombo ndipo ankaseka. "Bwanji, iwe unati iyo ikanati ivumbe zaka zana zapitazo! Agogo anga aamuna anandiuza ine kuti anakumva iwe kumtunda kuno ukuti iyo ikanati ivumbe, ndipo iwe ukumenyabe chidutswa chakale cha mtengo ichi kuno. Bwanji iwe siukuganiza bwino?"

Koma izo anali Mulungu akukonzekera kuti akatsimikizire lonjezo ndikukwaniritsa uneneri umene mneneri Wake anapanga. Zosazolowereka kwambiri! Mulungu akukwaniritsa lonjezo Lake kwa Nowa, pamene ena anali akuseka. Mulungu analinso akukonzekera kuti apange mbiri yakale kuti asonyeze kwa ena, ngakhale mpaka tsiku lino, kuti Iye amasunga Mawu Ake! Ziribe kanthu momwe zingawonekere zosakhala zenizeni, ndi zosaganizirika, Iye amasungabe Mawu Ake. Iye anali akupanga icho mwachitsanzo, kuchokera mwa bambo wachikulire amene ankagogoda pachombo chimenecho, kwa anthu

awa kuno mu America usiku uno ndi konse konse m'dziko. Ziribe kanthu zimene sayansi inena, zimene iwo anena izi, izo, kapena zina, Iye amasungabe Mawu Ake. Iye anali akupanga mbiri (history).

29 Nchiyani chinali chokopa tsiku lina.. Chinthu chosazolowereka chinachitika nkati mwachipululu, ndipo icho chinali chitsamba chimene chinali chikuyaka moto. Ndipo mneneri wothawa anali ataima pamenepo muchipululu. Iye sanamve konse liwu, iye sanamve konse phokoso, koma iye anayang'ana ndipo anawona chinthu chosazolowereka pamwamba pa phiri. Mulungu anali kuyesera kuti akope chidwi chake. Mofanana izo ziri lero!

Mulungu anali akukonzekera kuti akwaniritse Mawu Ake mwa mneneri Wake Abrahamu, "Mbewu yako idzakayenda zaka mazana anayi mudziko la chilendo. Ine ndidzakawatulutsako iwo ndi dzanja la mphamvu."

Ndipo Hye anali kumukonzekereza mwamuna kuntchitoyo, monga Iye anali kukonzeketsa chombo cha malo achitetezero kwaonse amene akanati akhulupirire. Mulungu anayatsa moto mu nchitsamba ichi, ndipo oweta nkhusa uyu, Mose, anati, "Ine ndingotembenukirako ndiwone chimene chinthu chachilendo ichi chikutanthauza." Ndipo pamene Iye anamufikitsa Mosepa chitsamba, Iye anayankhula kwa iye.

30 Chinali chiyani chokopa kumeneko mubwalo la Pilato, pamene oweta nkhusa uyu anaponyera pansu ndodo ndipo iyo inasanduka njoka? Mulungu akukwaniritse lonjezo lake kwa Mose. Chinali chiyani chokopa pa Dead Sea, pamene akavalo a Farawo onse anadabwitsidwa, pamene iwo anawona mphepo ikubwera pansu kuchokera kumiyamba ndikugawanitsa Nyanja yofiira kuchokera kumanja ndi kumanzere; ndipo gulu losauka la akapolo, akuyenda muntchito ya Mulungu anayenda kuwoloka apo panthaka youma? Chinali chiyani icho? Mulungu akusunga Mawu Ake. Kufa kunachokapo, anthu amoyo anawoloka; ndipo anthu akufa mwauzimu anayesera kuchita mowonera izo, ndipo anamira. Mulungu akukwaniritse uneneri ndi kupanga mbiri yakale. Icho chinali chokopa pa Dead Sea.

31 Chinali chiyani chokopa tsiku lachiwiri zitachitika izo, pa phiri la Sinai pamene anthu onse analamuliridwa kuti asagone ndi akazi awo, pamene iwo anafunsidwa kuti achape zovala zawo ndi kuti adziyeretse okha, ndikukasonkhana mozungulira phiri kumene mwamuna dzina lake Mose anati iye anakomana naye Mulungu mu lawi la moto? Ndipo Mulungu anali atanena kwa Mose, "Ine ndikuti ndibwere pansu pakati pa anthu. Ine ndikubwera kuti nditsimikizire chija chimeneIne ndinakuuza iwe,ndi Yemwe Ine Ndiri. Ine ndikuti ndiwasonyeze iwo kuti Ine Ndine Mulungu ameneyo." Icho chinali chokopa, Mulungu akukwaniritse Mawu Ake.

32 Chinali chiyani chokopa tsiku lina mumbiri yakale, kumene fuko linali litamuiwala Mulungu, kumene anthu anali atakhala achizolowezi ndi osayanjanitsika, kumene ansembe onse anali atapita ndi kachitidwe kamakono, aneneri ankalosera molingana ndi chifuniro cha ansembe? Ndipo mu tsiku limenero, monga mwachizolowezi, iwo anali naye munthu m'modzi yemwe amaganiza kuti anali otentheka. Iye ankayankhula za akazi odzipenta ndi chirichonse, ndipo iye anali mtundu wamunthu wasamvetseka. Ndipo munthu wachikulire uyu anali atabwera uko ndipo anati kwa amfumu, "Palibe ngakhale mame ati aitane... Kubwera mpaka ine nditawayitanitsa iwo."

33 Ndipo ife tikupeza kuti, ndiye, kuti iye anakazibisa yekha ndipo nathawa icho, ndipo iye anakabisala muchipululu kwina kwake. Amzakewo ankaganiza kuti mwina iye anali atafa ndi njala kapena anatayika; koma iye anakhala akudyetsedwa bwino kwambiri ndikumwetsedwa, naponso. Ndipo pano iye anali, atabwera pansu ndipo anati, "Kodi inu mukuona kuti ine ndiri naye PAKUTI ATERO AMBUYE? Tsopano, ngati inu simuli okhutitsidwa panobe, tiyeni tikwere pamwamba ndikukatsimikizira yemwe ali Mulungu," pakuti iye anali ndi masomphenya ena ochokera kwa Ambuye.

Iye anati, "Sankhani inu guwa, ndipo lipangeni ilo, ndipo - musankhe ng'ombe ndikuzipha izo. Ine ndipanga guwa la Ambuye, ndiponso ine ndiyika ng'ombe pa langa. Ife tonse tipanga nsembe, ndipo timulole Mulungu yemwe ali Mulungu ayankhe." Iye sakanati mwanjira iriyonse achite izo ngati Ambuye akanakhala kuti sanamuze iye; iye ananena choncho kenako, "Ine ndachita izi kwa... Zonse izi, mwakulamula kwanu Ambuye."

34 Koma nchiyani chokopa? Alinawo ansembe mazana anayi atayima pa phiri, ndi mfumu pa mwamba pamenepo mu galeta wake, ndi zida zake zonse ndi asirikali ataima mozungulira. Ndipo wachikulire uyu, waubweya, bambo wa nkhope yosaoneka bwino, wa mutu - wadazi, ndipo tsitsi likulendewera pansu pa nkhope yake, kachiduswa ka chikopa cha nkhusa atadzikuta nako mozungulira pa iye, ndi tsitsi pathupi lake lonse, atayima pa mwamba apo ndi ndodo pa dzanja lake, ndi nsupa ya mafuta mudzanja linalo; amene anangonena, zaka zitatu ndi theka ilo zisanachitike, "Sipakhala ngakhale mame ati agwe mpaka ine nditaitanitsa iwo," kutenga malo a Mulungu, ndi zinthu zonga izo monga kuwala ndi mithunzi ndi zonse zimene iwo amazikamba. "Ndipo apa otentheka wachikulire uja ataima pa mwamba apo pa phiri, nabweretsa anthu onse awa pa mwamba apo." Chinali chiyani chokopa chimenecho? Uyu anali Mulungu Akukonzekera kuti amutsimikizire mneneri Wake kuti akulondola. Izo anali Mulungu akukwaniritse uneneri Mulungu ndiponso akupanga mbiri yakale, akukwanilira Mawu.

35 Zaka mazana pang'ono zitachitika izo, uko kunali munthu atadzozedwa ndi Mzimu womwewo, ndipo iye anabwera kuchokera kuchipululu, osalumikizana ndi mabungwe aliwonse; ngakhale bambo wake anali munthu wabungwe, wansembe wadongosolo. Koma iye anabwera kuchokera kuchipululu, atavala chikopa chankhosa mozungulira iye, tsitsi pa nkhope yake yonse. M'malo moti ilo likhale lotuwa, ilo linali lakuda. Chiyani chokopa cha munthu uyu chimene chinakopa Yerusalemu yense ndi Yudeya? Ena aiwo anapita akuti, "Kuli munthu wakuthengo kumusi uko. Iye akuyesera kuti awamize anthu m'madzi ndani anayamba wamvapo chinthu chotero ngati icho?"

36 Ena anali achidwi, ndikumati, "Ameneyu ayenera kukhala ali Mesiya." M'modzi wa iwo anati, "Iye akhoza kukhala m'modzi wa aneneri." Iwo sankadziwa choti nkuganiza. Koma icho chinali chiyani? uyo anali Mulungu akukwaniritsa Yesaya 40, pamene iye anati, "Taonani..." Chimene Iye akanati adzachite mumasiku otsiriza, momwe Iye akanati adzatumizire wa ntchito wake ndi chimene iye akanati achite.

Ndiye ife tikupeza, masabata angapo zitachitika izo, bambo uyo pokhala otsimikiza nao kwambiri Uthenga wake, mpaka iye anati, "Pali wina waima pakati panu, yemwe nsapato zake ine sindiri oyenera kuzinyamula. Iye adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi Moto, monga ine ndikukubatzani inu ndi madzi."

37 Tsiku lina, mwamuna wamba wamng'ono, wapafupi usinkhu wazaka makumi atatu, anapita kumeneko ndipo anabatizidwa. Ndipo pamene munthu uyu anabwera, uko kunali kukopa kotero ndi mneneri, mneneriyo anachita mwachilendo tsiku limenelo. Gulu silikanakhoza kuchitira mwina pakuona zochitika za mneneri ameneyo. Pamene iye anali kutsutsana ndi ansembe kutsidya kwa mtsinje.

Iwo anati, "Mulungu anamanga guwa ili. Mulungu anatiuza ife kuti tizichita izi. Mose ndi mneneri. Ife timamukhulupirira Mose. Nsembe sizizathetsedwa konse."

Ine ndikukhoza kumumva Yohane akuyankha mobwezera, anati, "Kodi inu simunawerenge m'Malemba chimene Daniele mneneri ananena, 'Nsembe za patsiku zidzathetsedwa'? Ndipo ora limenelo lafika! Kodi inu simunawerenge zimene Yesaya ananena mumutu wa 40, 'Liwu la ofuula muchipululu, konzani njira ya Ambuye'? Pali mauneneri awili a ine. Ndipo chinthu china, kodi inu simunazindikire mneneri wathu zaka mazana anai zapitazo, Malaki, pamene Iye ananena mu mutu wa 3 ndipo anati, 'Taonani, ine ndituma mtumiki wanga wapatsogolo pa nkhope yanga, kuti adzakonze njira'? Kodi inu simukudziwa kuti izi zikukwaniritsa uneneri?" uneneri unali ukukwaniritsidwa.

38 Ndipo pafupi nthawi imeneyo mneneri anatembenuka ndipo anati, "Taonani, alinkudza Mwanawankhosa wa Mulungu amene ati achotse tchimo la mdziko!" Tsopano nchiyani chokopa? Izo zinasintha kuchokera kwa mneneri kupita ku uneneri wake.

Tsopano zindikirani, zimene zikufika pochitika. Apa pakubwera munthu wamba, opanda wina omudziwa, mwana wampala matabwa, kubwera akuyenda mu madzi. Pamene Yohane, mneneri wankulu, anati, "Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi inu. Bwanji inu mukubwera kwa ine?"

Iye anati, "lolani izo zikhale chomwecho. Koma, monga mneneri ndi Mawu, izo zikutikhudza ife kuti tikwaniritse chilungamo chonse."

Chotero iye anamvetsa kuti nsembe inayenera kuti itsukidwe isanati iperekedwe, ndipo iye anam'batiza Iye.

39 Tsopano pali chokopa china chimene chikuchitika pamene Iye anatuluka kuchokera mmadzi. Mneneri uyu amene anakhala omvera kwambiri kuti alengeze m'badwo wake ndi nthawi, iye anayang'ana mwamba ndipo iye anaona miyamba itatseguka. Iye anaona Mzimu wa Mulungu monga nkunda, ukutsikira pa Iye, ndipo liwu linati, "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa mwa Iye ndikondwera." Mulungu anali akutsimikizira uthenga wa mneneri, umene unali kukopa tcheru pa Yordani.

40 M'bale anayimba kanthawi kapitako, kapena iye anayenera kuti ayimbe, "Pa phiri kutaliko panaima mtanda wakale okhukhudzidwa." Nchiani chokopa pa phiri la Kalvare? Pamene ife tikuwona kuti dziko la chipembedzo linali litamutsutsa Iye ndipo boma la chi Roma linali litamuweruza Iye kuti afe ndipo apa Iye anali atapachikidwa pakati pa mbala ziwiri, waludzu wofuna kumwa, magazi akuyenderera kuchokera muthupi lake ndi uyo wapachikidwapoyo akulira, "Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, mwandisiyiranji Ine?" Ndipo anthu achipembedzo ataima pamenepo akuyang'ana paizo, sankadziwa kuti uneneri wachipangano chakale unali kukumanizidwa apo pomwe pa Kalvare nthawi imeneyo.

Davide mwiniwake analemba, anachita... Analowa mu Mzimu monga aneneri onse, iye ankachita ngati ameneyo anali Iye. Davide analira, muSalimo ya 22, "Mulungu wanga, Mulungu wanga, chifukwa chiyani inu mwandisiya ine? Mafupa Anga wonse andipenyetsetsa ine. Iwo alasa manja Anga ndi mapazi Anga." Davide, akuyankhula ngati ameneyo anali Iye. Ndipo ameneyo sanali Davide, ameneyo anali Khristu mwa Davide.

Ndipo apa uneneri womwewo unaperekedwa, wa aneneri osiyana onse unali ukukwaniritsidwa pa phiri

la Kalvare. Ndichiyani chokopa pa phiri? Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake.

41 Chokopa china chinali pa phiri, chinali pa Tsiku la Pentekoste, pamene onse aiwo anali pamwamba apo muphwando la chipembedzo, ankaganiza kuti anali atathana nawo otentheka onse. Iwo anali asanamve kuchokera kwa iwo kwa masiku khumi. Zonse mwa dzidzidzi, ngati chisa cha njuchi iwo anamwazikira kunja pamwamba pa nyumba, kupita m'misewu, akufuula ndikuchita mopitiriza.

“Kodi ichi nchiani? Ichi chikutanthauza chiani? Kodi anthu onsewa aledzera?”

Penyani! Ndipo mneneri anayimirira pakati pawo, monga kachitidwe ka mneneri kanayenera kukhala kali, ndipo anati, “Inu amuna aku Israeli ndi inu okhala mu Yudeya, mu Yerusalemu, lolani ichi kuti chidziwike kwa inu, ndipo mvetserani mawu anga. Awa sanaledzere monga inu mukuganizira kuti iwo ali. Koma ichi ndichija chimene chinayankhulidwa ndi Ambuye kupyolera mwa Yoweri, Mneneri, 'Zidzafika pochitika mu masiku otsiriza, Ine ndidzatsanuirira Mzimu wanga pa mnofu uli wonse.’” Icho chinali chokopacho.

42 Anthu achipembedzo, atamupachika kale Kalonga wa Moyo, ndichirichonse. Komabe sanaliwone lonjezo lakudza kwa Mzimu Woyera. Chokopa, “Ndindani uyu? Ichi chikutanthauza chiani? Ndi chiani chavuta ndi anthu amenewo?”

O, mai! Ndizofanana lero. Ife tilambalala zambiri za izi kuti tibweretse izo ku ora lino chinthu chofanana chiripo lero. Chinthu chomwecho chikuchitika. Funso lomwero likufunsidwa. “Chiphokoso chonsecho ndi chachiani?” Kuyang'ana chokwera - ndi - kutsika mu nsewu, magalimoto ochokera ku Michigan mpaka ku Florida, wochokera ku Main mpaka ku Califonia. M'mawa uno pamene ine ndinali kuyendetsa, kapena atapitirira kumene masana, ife tinali kupita ndi msewu, mkazi wanga ndi ine tinali kuyang'ana pa misonkho pa galimoto. Ndi pamene ine ndinalingalira za mutu uwu. ”

izi zikutanthauza chiani?”

Basi monga izo zinanenedwa, “Kumene kwafa nyama, kumeneko mphungu zikasonkhana”!

43 Ine ndinati kwa mkaziwanga, “Okondedwa, iwe ukukumbukira usiku wotsiriza pamene ine ndinali kutsanzika kwa chirichonse chimene chinali chokondedwa kwa ine Pa dziko la pansu, ndikupita kuminda kuti ndikayambe china chake chimene Mulungu ananena ndichite? Iwe unaimba nyimbo ija.”

O, adzachokera kummawa ndi kumadzulo,

Adzachokera kumaiko akutali,

Kudzadya phwando ndi mfumu yathu,

Kudzadya monga alendo Ake;

Ndi odala bwanji amwenda mnjira awa!

Kuwona nkhope yake yowala

Yowala ndi chikondi cha Umulungu;

Odala ogawana nawo zachisomo chake

Monga ngale mukorona wake ife tidzawala.

44 Ndicho chimene chokopa chiri. Mbewu yokonzedweratu ya Mulungu omwe sangakhoze kuchita chinthu chirichonse koma kuwatsatira iwo, zikutanthauza mochuluka kuposa moyo kwa ife. Tengani miyoyo yathu, koma inu musati mutenge icho. Nchiyani chimene chiri chokopa? Mulungu, mwachizolowezi, akukwaniritsa Mawu Ake Iye akukwaniritsa mawu Azakaliya kachiwiri, a mneneri Zakaliya.

Pamene ine ndinawerenga ndime ya 9 kanthawi kapitako, pamene Yesu analowa mukachisi Wake, atakwera... Kapena anakalowa mu Yerusalemu, atakwera ka buru kakang'ono, koyera, uneneri unakwaniritsidwa umene Zakaliya ananena. Ndi izi apa, “Sangalalani kwakukulu, O, ana akazi a Zion. Fuulani, O, ana akazi a Yerusalemu. Taonani, mfumu yanu ikudza kwa inu; Iye ndi olungama, ndipo alinacho chipulumutso; otsika, atakwera kaburu, ndi pamwana wa phongo wa buru.” Ndicho chimene chinali chokopa kuYerusalemu, kulikulu la chipembedzo.

45 Tsopano ife tikuona chochitika cha tsiku - lotsiriza! Tiyeni tingotembenuza masamba angapo, mu Zakaliya, kuti tiwone zimene iye ananena pa izo. Tiyeni titembenuzire kumeneko ndiye kwa masiku otsiriza. Uwo unali m'badwo wapakati; tiyeni titembenuzire tsopano kumasiku otsiriza. Ndipo titembenuzire ku Zakaliya mutu wa 14, ndipo kuyambira ndime ya 4. Ndipo mvetserani! Ndipo ife tikuti tiwerenge chotsika gawo la Malemba, pafupi ndime zisanu ndi zinai kuyambira 4 mpaka 9 mvetserani mwa

tcheru. Ndipo izo zikunenera zakudza kwake, masiku otsiriza mvetserani mwa tcheru tsopano. Izi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndiwo Malemba, Zakaliya 14. Kumbukirani Zakaliya 9, chimene iwo ananena? Ndipo iwo sanadzizindikire izo. Tsopano nchiani izo lero? Zakaliya 14, akuyankhula zakudza kwake.

Ndipo mapazi ake adzaima mutsiku limenelo pa Phiri la Azitona, kachiwiri limene liri kuyandikira Yerusalemu cha kum'mawa pa Phiri la Azitona Padzang'ambika pakati pake cha kum'mawa ndi cha Madzulo ndipo padzakhala pali chigwa chachikulu Kwambiri;... Gawo la Philiro lidzakhala litasunthira Cha kumpoto, chigawo.... Cha kumwera.

Ndipo inu mudzathawira muchigwa cha mapiri; Pakuti chigwa chamapiri chidzafika kuchokera ku Azali: eya inu mudzathawa, monga inu munathawira mumasiku a chivomezi mumasiku a Uziya mfumu ya a Yuda: ...

46 Chivomezi china chikugawaniza motsegula dziko lapansi ngati inu mukufuna kuti mutsatire Malemba apa, zindikira mundime ya 5 iyi, izo zikunena kuti kugawanika kwa phiri la Azitona kuli chifukwa cha chivomezi, ndipo izi zikutsimikizidwa ndi Yesaya 29:6 ndi Chibumburutso 16:9. Ndendende! Nchiyani icho? Mneneri yemwe uja ananena za kubwera kwake koyamba, "Monga mumasiku achivomezi." Mukuona chimene chivomezi chimene chikuchita? Mukuona kunenedweratu kwa izo?

.... Ndipo Ambuye Mulungu wanu adzadza, ndiwoyera Ake onse ndi iye. Ndipo izo zidzafika pochitika mutsiku limenelo, (Aleluya) mu tsiku limenelo, kuti kuwala sikudzakhala kowoneka, kapena mdima: Koma ilo lidzakhala tsiku limodzi ndi Tsiku Limodzi limene liti lidzadziwike kwa AMBUYE, osati Usana, kapena usiku: koma zidzafika pochitika, kutiMunthawi ya madzulo kudzakhala kuli kuwala. (O Mulungu!)

47 "Kudzakhala kuli kuwala pafupi nthawi ya madzulo," mneneri yemweyo. Ndipo anthu ali akhungu! Ndichiyani chokopa? Tiyezi tiwerenge ndime zina zingapo.

Ndipo zidzakhala mu tsiku limenelo kuti madzi amoyo adzatuluka kuchokera ku Yerusalemu; theka la iwo chaku Nyanja yakale, ndi theka.... Chaku Nyanja yakumbuyo: muchirimwe ndi... Dzinja zidzakhala ziri (Uthengawabwino uli kuperekedwa; onse a Yuda ndi amitundu.)

Ndipo YEHOVA adzakhala ali mfumu pa.... dziko lapansi: mu tsiku limenelo, ndipo kudzakhala kuli Ambuye mmmodzi ndi Dzina lake limodzi.

Kudzakhala kuwala kunthawi ya madzulo, (kulondola)

Njira ya ulemelero mudzaipezadi;

Munjira ya madzi muli mkuwala lero,

Kumizidwa mu dzina lofunika la Yesu.

Ana ndi aakulu, lapani machimo anu,

Mzimu Woyera udzalowamo ndithu;

Kuwala kwa madzulo kwabwera,

Zowona Mulungu ndi Khristu ndi m'modzi

Mukuona pamene ife tiri?

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,

Zizindikiro zimene aneneri athu ananeneratu;

(chivomezi chija kwa a mitundu ku tsiku lotsiriza)

Masiku amitundu awerengedwa, ndi zoopya zitachuluka;

bwerani, O, omwazika, kwanu.

Inu amene mwathamangitsidwa kunja, ndi malikasa awa amene akunyamulidwa pangolo zatsopano, tulukaniko uko imfa isanakukantheni inu. Mulungu watsimikuzira izo. Izo zikhala momwemo.

48 Tiyezi ife titembenzire Mulemba lina muchipangano chakale, Malaki mutu wa 4, ndikuwerenga mutu 4 waung'ono uwo.

.... Taonani, tsiku likudza, limene liti lidzawotche monga ng'anjo; ndipo onse onyada, eya, Onse amene achita moipa, adzakhala ngati ziputu:

Tsopano, izi sindizo Ndizo Malaki 3, kunali kudza koyamba, tsopano apa pali kudza kotsatira. Ngakhale Dokotala Scofield pano, ine ndithudi sindimagwirizana naye muzolemba zake zapansi, koma iye

wazifotokoza izo apa molondola. "Kutumidwa kwa Yohane," ku Malaki 3; ndi, "kudza kwachiwiri kwa Khristu," ndi Eliya zisanachitike..

.... Onse onyada adzawotchedwa, atero Ambuye wamakamu ndipo sadzawasiyira iwo ngakhale muzu kapena nthambi. (alikuti Gehena "Wamuyaya" ndiye?)

Koma kwa inu amene mumaopa dzina langa dzuwa la chilungamo lidzakutulukirani ndi misonkhano ya machiritso, machiritso mu mapiko ake;... Inu mudzayenda, ndi kukula ngati ana ang'ombe a mkhola.

Ndipo inu mudzapondereza pansi oyipa;... Iwo adzakhala mapulusa pansi pa zidendene za mapazi anu mu tsiku limenelo lomwe ine nditi ndidzachite izi, atero AMBUYE wa makamu.

Kumbukirani... Lamulo la Mose wantchito wanga, lomwe Ine ndinamulamulira... Iye mu Horebu kwa Israeli yense,.. Malangizo ndi chiweruzo.

49 Pano pali kudza kwa Eliya.

Taonani, Ine ndidzatumiza kwa inu Eliya mneneri....

Lemba lotsekera lotsiriza la Chipangano Chakale!

.....Ine ndidzatumiza kwainu Eliya mneneri lisanadze tsiku lija lalikulu ndi lowopsya la AMBUYE:

Tsopano, izo sizikanakhoza kukhala Yohane. Ayi. Mukuona, dziko linali lisanawotchedwe ndipo olungama nkumayenda pa oyipa. Mukuona? Ayi, ayi.

.... Lisanadze tsiku lalikulu ndi loopysa la AMBUYE:

Ndipo iye adzatembenuzira mitima ya Atate kwa ana, ndi mitima ya ana kwa Atate, kuti Ine ndingadze ndikukantha dziko lapansi ndi themberero.

Zindikira kulondola kwa Mzimu Woyera kuti iwo sukanati usokoneze kudza kuwiri uko kwa Eliya. Malaki 3, anati "Taonani, Ine ndikutumiza mtumiku wanga patsogolo pa nkhope yanga." Yesu anafunsidwa za Yohane; Iye anati, "ngati inu mungakhoze kuzilandila izo, uyu ndi yemwe mneneri anati, 'Ine ndidzatumiza mtumiki wanga patsogolo pa nkhope yanga.' Ameneyu ndi Eliya yemwe anali woti adze." Malaki 3.

50 Zindikilani Lemba likupereka izo molondola. Tapenyani chimene izi ... kuti asonyeze ... iwo amene akufuna kuti akhulupirire, iwo amene akufuna kuti awone. Kumbukirani, Yesu analekeza mkati mwa Lemba chifukwa gawo la ilo linakwaniritsidwa pamenepo, linalo pakudza kwake kwachiwiri? "Kuti alalikire chaka chovomerezeka cha Ambuye, kudzamanga osweka mtima," ndipo analekeza; osati "Kubweretsa chiweruzo kwa Amitundu" mpaka kudza kwake kwa chiwiri.

51 Zindikirani Lemba ili pano likuyendera limodzi ndi ilo. "Ndipo iye, Eliya, adzatembenuzira mitima ya atate kwa ana." (Tsopano akuyankhula za Malaki 4, musati muzisakanize izo, kapena Malaki 3.) Yohane, Eliya, yemwe anadza mumasiku kusanafike kudza koyamba kwa Khristu, anatembenezira mitima ya makolo akale ku uthenga wa ana, uthenga watsopano.

Tsopano penyani. "Ndi mitima ya ana kwa makolo." Mukudza kwake kwa chiwiri, mumasiku otsiriza, iye akutembenezira anso ku chikhulupiliro cha utumiki kachiwiri. Mukuna momwe mwangwiro Malemba akufotokozera?

Uko kunali kutha kwa chipangano chakale, chipangano chakale. Tsopano ife tikuwona kuti pali kuwala mu nthawi yamadzulo. Ndipo nchiyani icho? Iyo ndi nsonga, phili la Treetop.

52 Monga ine ndinanena m'mawa uja, ife tabwera kudutsa zipembedzo, kudutsa (osati mtengo wa lalanje) monga ine ndimaukamba m'mawa uwu, koma ife takhala nacho chipatso cha mpesa, mandimu, mitundu yonse ya zinthu zina zimene sizinali monga pachiyambi nkomwe. Koma pambuyo.... Musati muphonye izi. Pano izo zikubwera. Pambuyo pa zipembedzo zonse zitaseweredwa, izo zinalibe kuwala kulikonse pa kuyamba nazo, padzakhala tsiku limene silingakhoze kutchedwa usana kapena usiku.

Kodi iwo akuchita chiyani? Kodi iwo akuchita chiyani? Kodi e - ndimu limachita chiyani pa mtengo wa lalanje? Ilo limatenga moyo wa pachiyambi wa lalanje umene ukukwera kuwupotoza iwo kudzera mu ndimu. Ndicho chimene zipembedzo zachita kwa Mawu a Mulungu, zawapanga Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu mwa miyambo yawo. Ndizo PAKUTI UKUTERO MZIMU WA AMBUYE. Iwo abala mandimu, zipatso za mpesa - osati malalanje.

53 Koma kodi mneneri anati chiyani? M'modzi yemweyo yemwe anati kwa phunziro lathu usiku uno, "Sangalalani, O ana aakzi a Yerusalemu, fuulani mokweza, ana aakazi a Zioni, pakuti Mfumu yanu ikudza kwa inu, wofatsa ndi wodzichepetsa, atakhala pa mwana wamphongo wa buru," Zindikirani mneneri yemwe uja anati, "Idzafika nthawi ya kucha." Dzuwa kutumizidwa pa dziko lapansi kuti likachetse chipatso. Nchifukwa chiyani icho sichimakhoza kucha? Mulibe chipatso umo kuti chiche. Koma moyo

ukupitabe patsogolo.

54 Iwo unabwera m'mwamba kupyolera muchipatso cha mpesa, kuti ukhale lalanje, unadzapeza kuti unachita bungwe; iwo unali chipatso cha mpesa. Iwo unapita kachiwiri, iwo unatulukira nthawi imeneyo ndimu. Unapitanso kachiwiri, iwo unatulukira chinthu china chake. Ndipo kumapeto, pa nsonga ya mtengo, iwo unatulukira mu manyumwa, yomwe ili theka lalanje, theka ndimu; mtundu wosakanizika, chinthu chopotozedwa; unafika ku chosokonezedwa, kumakhala moyo wochokera mu mtengo womwewo; mankhusu, "Pafupi kuti anyenge Osankhidwa." Kumawoneka ngati lalanje, koma ilo lisali.

"Koma kudzakhala kuli kuwala," pamene iwo akukula kupitirira bungwe. Pamene iwo udzadzutsa kupyola bungwe, iwo nuchita maluwa kachiwiri, iwo udzabala malalanje monga iwo unali pamene iwo unkapita mu nthaka, ndiyeno kudzakhala kuli Kuwala.

Kodi chokopa ichi ndi chiyani; nchiyani chikuchitika ichi? Kukwaniriritisa Mawu a Mulungu. Ziripo mboni ziwiri za Chipangano Chakale, zoti izi zikanati zidzachitike.

55 Tiyeni titenge Yohane 14:12, wa Chipangano Chatsopano, Yesu anati "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iye adzazichitanso"

Ndipo, mu Luka 17:22 mpaka 30, Iye anati. Monga izo zinali mumasiku a Loti, Sodomu asanawotchedwe, chomwechonso izo zidzakhala ziri pakubwera kwa Mwana wa munthu, tsiku limenelo pamene Mwana wa munthu akhala akuwululidwa.

O, tangoyang'anani pa Malemba! "Mwana wa munthu," Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, anakula kupitirira zipembedzo, anakula mpaka munsonga ya mtengo. Kodi Iye ananena chiyani mu Yohane 14, kapena 15? "Nthambi iriyonse imene ili mwa Ine, imene sibala chipatso, iyo idzadulidwa ndi kutsadzidwa, kuponyedwa mu moto ndi kuwotchedwa. Koma nthambi iliyonse imene iti idzabale chipatso, iyo idzayeretsedwa."

56 O, kudzakhala kuli mvula yoona ya nyundo ndi ya masika mumasiku otsiriza pa gulu laling'ono ilo limene likudza ndi Iye pa buru wam'ng'ono uyu, ofatsa ndi wodzichepetsa, osati chip - Kapena chipembedzo, akufuula, "Hossana kwa mfumu ikudza mu Dzina la Ambuye!" Vuto nchiyani lero? Nchiyani chokopa pa phiri?

57 Si kale litali, nditaima pa guwa ili, izo zinanenedwa ndi Mzimu Woyera, "Tsiku lidzadza kuti pamene iwo atadzakhomerere pansi chikhomo patsogolo pa nyumba yako; iwo adzasuntha chipata chako. Chotero, kuti, iwe udzazilambalale izo, osakhala uli wokwiya." Ine ndinawona chipata changa chikuphwasulidwa ndipo chitakaikidwa pambali pa phiri. Ine ndinawona phili patsogolo kwa ine, lonse litakumbidwapo, ma bolodi ndi zinthu ziri apo pamene chinachake chinali chitadziphwanya icho. Iye anati... Ine ndinayang'ana, ndipo apo panali Ricky wam'ng'ono yemwe anali atakwera pamene ndipo anachichotsapo chipata chimenecho, anachita izi. Ine ndinati, "bwanji iwe sunandiuze ine?" Iye anayamba kundichenjerera, ndipo ine ndinayenera kum'menya iye. Ndipo pamene izo zinatero, ine ndinati, "Ine sindinachite izi chichokereni mu bwalo la nkhonya, koma ine ndikungofuna kuti iwe udziwe," ndipo pamene ine ndinamusasantha nayo imodzi. Ndipo pamene ine ndinamugwetsera iye pansi, ine ndinamudzutsa iye kachiwiri ndikumugwetsera iye pansi kachiwiri. Ine ndinamudzutsa iye, nthawi zitatu kapena zinai, ndiyeno ndinamukankhira iye pa mwamba pa phiri. Chotero ndiye ine ndinapita chakumeneko, ndipo ine ndinati, "izo sizabwino." Ndipo ine ndinadzutsa iye ndipo ndinagwedeza manja ake, ine ndinati, "ine sindinakukwiire iwe, koma iwe ndimangofuna kuti iwe udziwe iwe sungamayankhule choncho kwa ine." Ndiyeno pamene ine ndinatembenuka ndikubwereranso, Mzimu Woyera unali utaima pamene pachipata unati, "tsopano udzazilambalale izi. Pamene chikhomo icho chidzakhomeredwa pansi, udzatembenukire cha kumadzulo."

Buku iri ndi chirichonse chimene ine ndikuchisowa,

Buku rli ndi chakudya chabwino. (Njira imene imasonyeza momwe ndingapite

Molambalala vuto langa. Amenii!

Ndipo Buku limenelo ndi Mawu ndipo Mawu amenewo ndi Mulungu, lambalala mavuto ako, ilo lidzakuwuzwa iwe choti uchite.

58 Zaka zitatu zapitazo ine ndinamumva nzanga wa ine, wopima malo mu mzinda, amakhala kumusi kwa nsewu kuchokera kwa ine, akukhomerera chikhomo pansi. Ine ndinapita kumeneko ndinati, "Chavuta ndi chiyani, Mud?" mwana wa bambo King, nzanga wodziwana naye.

Anati, "Billy, iwo akuti akuze nsewu uno."

Inu nonse mukumbukira. Ine ndinati, "iwo mwina udzakhala mulantho." Ine ndinamuuza m'bale Woods, ine ndinati, "gwiritsa malo ako. Mwina mwake mulatho umenewu ubwera kudzadzutsa pano, china chake." Njirayo inali itaphwasulidwa; njerwa, miyala, zitaponyedwa paliponse chirichonse. Chotero iye anati.... Ine

ndinati, "gwilitsa malo ako."

Ndiye pamene bambo King anandiuza ine kuti izo zimati zichitike. Ine ndinakalowa umo, ndinakanena kwa mkazi wanga atakhala pamenepo, "Wokondedwa, pali china chake chinalembedwa chokhudza. Ndi-PAKUTI ATERO AMBUYE, kwina kwake."

59 Ine ndinakalowa ndipo ndinakatenga buku langa, ndinayang'na nkatimo, ndipo ilo linati, "Izo zidzafika pochitika..." Zaka zisanu ndi zitanu mtsogolo!

Ndiye pamene ine ndinayang'ana pa izo, ine ndinati, "Ndinthawi tsopano wokondedwa, ife tiyenera kutembenukira kumadzulo."

Masiku awiri zitachitika izo, nditayima muchipinda pafupi teni koloko m'mawa wina, ine ndinapita mu Mzimu wa Mulungu. Ine ndinawona kuwundana kwakung'ono, kuja kwa nkunda zikuwuluka, ndiyang'ana pambalame zazing'ono izo. Inu mukukumbukira izo. Ine ndinawona Angelo asanu ndi awiri mumawonekedwe a pilamidi, akubwera kuthamangira kwa ine. Anati, "Tembenukira chakudzulo, pita ku Tucson ukakhale mailosi makumi anai cha ku mpoto. Ndipo iwe udzakhala ukuchotsa chisoso," kapena namutu wa ng'ombe, iwo amazitcha izo uko, "kuchokera pa zovala zako."

60 M'bale Fred Sothmann wakhala kumbuyo uko akuyang'ana pa ine pakali pano, anali kumeneko m'mawa umenewo. Ine ndinali nditaiwala za izo.

Ine ndinati, "Kuphulika kunachita monga chivomezi, kumene kunagweddeza pafupi chirichonse chimene chinalipo mu dzikolo. Ine sindikuona momwe munthu akanati apulumukire ku icho." Ine ndinachita mantha. Ine ndinayima ku Phoenix, inu nonse amene mukumvetsera usiku uno mundichitire ine umboni. Ine ndinalalikira pa ulaliki, Mabwana, Ndi Nthawi Yanji Ino? "Kodi ife tiripati?" Ine ndinapita kumadzulo. Ambiri a inu pano muli nayo tepi imeneyo, ambiri a inu pano munazimva izo zikunenedwa, chaka kapena mochuluka izo zisanachitike.

61 Ine ndinapita kumadzulo ndikudabwa chimene chikanati chichitike. Tsiku lina ndinalandira kuitana kuchokera kwa Ambuye. Ine ndinamuuza mkazi wanga, ine ndinati, "Wokondedwa, ine ndiri.... Mwina ntchito yanga yatha." Ine sindinali kudziwa. Ine ndinati, "Ine Mulungu mwina wathana ndi ine tsopano ndipo ine ndikhala ndikupita kwathu. Iwe upite ukamutenge Billy, uwatenge ana. Mulungu akupangira njira iwe, mwina mwake. Pitirira ndikukhala moona kwa Mulungu. Ona kuti ana atsirize sukulu, uwalere iwo mwa malangizo a Mulungu."

Iye anati, "Bill, iwe sukudziwa kuti izo ndi zoono."

Ine ndinati, "Ayi. Koma munthu sakanakhoza kupulumuka pa izo."

M'mawa umodzi Ambuye anadidzutsa ine, anati, "Pita uko Mu Sabino Canyon." Ine ndinatenga chidutswa chapepala ndi Baibulo langa.

Mkazi wanga anati, "Kodi iwe ukupita kuti?"

Ine ndinati, "sindikudziwa. Ndikuwuzwa iwe ndikabwerako."

62 Ine ndinapita pa mwamba mu Canyon, ndinakwera pamwamba pamene mphungu zinali kuwuluka mozungulira. Ine ndinali kuyang'ana agwape ena atayima pamenepo. Ine ndinagwada pansu kuti ndipemphere, ndipo ndinakweza m'mwamba manja anga, ndipo Lupanga linakhudza dzanja langa. Ine ndinayang'ana pozungulira. Ine ndinaganiza, "Nchiani chimenecho? Ine sindinasokonezeke. Apa pali Lupanga ilo m'dzanja langa; lowala, kung'anima, ndikunyezimira mudzuwa." Ine ndinati, "Tsopano, kulibe anthu mamailosi kuchokera kwa ine, kutali kuno mu Canyon iyi. Ilo lingachokere kuti?"

Ine ndinamva Liwu, linati, "Ilo ndi Lupanga la a Mfumu."

Ine ndinati, "Mfumu amamupatsa munthu udindo ndi Lupanga."

Iye...Liwulo, linabwerera, linati, "Osati lupanga la mfumu, koma, 'Lupanga la a Mfumu,' Mawu a Ambuye." Anati, "Usawope ayi. Ndichikoka chachitatu basi. Ndiko kutsimikizira kwa utumiki wako."

63 Ine ndinali kupita kokasaka ndi mzanga, osadziwa chimene chikanati chichitike. Ndipo wina wake anandiitana ine, yemwe ankanditsutsa ine zachithunzi chija cha Mngelo wa Ambuye, yemwe anachijambula icho. Ine ndinapita ku Houston pazokhudza mwana wake, pakuti iye anali kupita mumzere wa imfa ndipo anali woti akaphedwa mumasiku pang'ono, ndipo iye anakomana nane ine m'menemo ndipo anatambasula mikono yake kundikumbatira ine, anati, "Taganizani, munthu yemweyo ine ndimamutsutsa akubwera kuti adzamupulumutse mwana wanga yekhayo!" Bungwe la za umunthu linandipatsa ine chimene iwo amachitcha Oskara, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuti muchitche icho, chifukwa chopulumutsa moyo.

64 Ndiye ife tinabwerera, ine ndinapita pamwamba pa phiri kuti ndikasakeake. Uko, m'bale Fred ndi ine,

m'mawa wina pamene ndinatuluka, ndipo ine - ine ndinali nditapeza kale nguluwe yanga, ndipo ine ndinayang'ana ndipo ndinawona kumalo kumene izo zimapita. Ine ndinati, "M'bale Fred, pita ku phiri ilo molawila tsopano pafupi kutulukira kwa tsiku, ndipo ine ndipita palinalo. Ine sinditi ndiwombere panguluweyo, sindiipha iyo. Koma ngati izo ziyamba kubwerera kumbali iyi, gulu ilo, ine ndikawombera kutsogolo kwa izo ndikuzithamangitsa izo kuti zibwerere."

65 M'bale Fred anapita uko ndipo kunalibe nguluwe. Iye anagwedeza kwa ine ndipo ine ndinawona. Ine ndinapita M'musi mu Canyon, mapompho ena aakulu, dzuwa linali likutuluka kumene. Ine ndinabwera kuzungulira mbali yina ya phiri, osalingalira kanthu zokhudza mauneneri. Ndinakhala pansi, kuyembekezera, kupumula; ine ndinaganiza, "Nchiyani chinachitika kwa nguluwe zija?"

Ine ndinanyamula yanga... Ndinakhala pansi monga amachitira amwenye, inu mukudziwa, kupingatsitsa - miyendo. Ine ndinayang'ana pa mwendo wanga wa ovolosi, ndipo apo panali chisoso. Ine ndinachichotsa icho. Ndipo ine ndinati, "Izo ndizachilendo! Ine ndili kuno, pafupi mailosi makumi anai kumpoto cha ku m'mawa kwa Tucson. Apo pali mnyamata wanga wang'ono Joseph wakhala uko akundiyebekeza ine." Ndipo pamene ine ndinayamba kuti ndidziyang'ana ine ndinawona gulu la nguluwe zikubwera uko pafupi mayadi chikwi zikubwera kwa ine, pamwamba pa phiri, ine ndinaponyera chisosocho pansi. Ine ndinati, "Ine ndikazipeza izo. Ine ndipita ndikamutenge M'bale Fred, ndipo ine ndipachika chidutswa cha pepala kuti ndimudziwitse njira yoti adzere ku Ocotillo muno, ndipo ife tikamupeza M'bale Fred."

Ndipo ine ndinauyamba kukwera phiri ndikuthamanga dzolimba monga ine ndikanathera kumbali inayo. Zonse mwadzidzi, ine ndinaganiza kuti wina wake anandiwombera ine. Ine sindinayambe ndamvapo kuphulika koteroko; iko kunagwedeza dziko lonse. Ndipo, pamene iko kunatero, ataima patsogolo pa ine anali Angelo asanu ndi awiri mukuwundana.

66 Ine ndinapezana naye M'bale Fred ndi iwo kanthawi kotsatira.

Anati, "Chinali chiyani chija?"

Ine ndinati, "chinali chimenecho."

"Muchita chiyani inu?" "Kubwerera kunyumba. PAKUTI, NDI ATERO AMBUYE, Zinsinsi zisanu ndi ziwiri zimene zakhala zitabisika mu Baibulo zaka zonse izi, zipembedzo izi ndichilichonse, Mulungu akuti akatsegule zinsinsi zisanu ndi ziwiri zimenezo kwa ife muzisindikizo zisanu ndi ziwiri."

Apo panali nkombere uja ukukwera kuchokera pa dziko, ngati kupangika kwa nthunzi. Pamene iwo unatero, iwo unakwera pa mwamba mu phiri, unayamba kupanga nkombere ukunka chakumadzulo, kuchokera komwe iwo unachokera. Sayansi inaupeza iwo patapita kanthawi, mailosi makumi atatu m'mwamba ndi mailosi makumi awiri ndi asanu chopingasa, ndendende basi mwa nkombere wa piramidi.

67 Ndipo tsiku lina, nditaima pamenepo, ndinatembenezira chinthunzicho kunja, ndipo apo pali Yesu monga Iye anali m'mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mpingo, atavala wigi yoyera, akusonyeza Umulungu Wapamwamba. Iye ndi Alefa ndi Omega; Iye ndi Oyamba ndi Otsiriza; Iye ndi Oweruza Wapamwamba wa Umuyaya wonse, akuima pamenepo, kukatsimikizira Uthenga wa ora lino. Ndipo kudzakhala kuli kuwala cha mu nthawi ya madzulo! Kodi zonsezo ndi zachiani? Chinali chiani icho?

68 Ine ndinapita chakumadzulo. Pa phiri lomwelo, ndikudutsa apo ndi Banks Woods kumeneko, anati, "Ponyera mwala m'mwamba. Nena kwa bambo Woods, 'PAKUTI ATERO AMBUYE, iwe uwona Ulemelero wa Mulungu'."

Tsiku lotsatira lomwe, nditaima pamenepo, kamvuluvulu anabwera pansi ndipo anawaphulitsa mapiri. Miyala inadula nsonga za mitengo. Pafupi mapazi atatu kapena anayi pamwamba pa mutu wanga. Kunapanga kuphulika kutatu kwa kukulu, ndipo abale anabwera kuno akuthamanga. Analipo pafupi amuna khumi ndi asanu ataima pamenepo, alaliki ndi china chilichonse. "Kodi chinali chiyani icho?" iye anati, "Kodi chinali chiani icho?"

Ine ndinati, "Chiweruzo chikukantha Gombe la kumadzulo."

69 Pafupi masiku awiri zitachitika izo, chivomezi chinali pafupi kuti chimize Alaska. Kuwala uku ndichiyani pa mwamba pa phiri la Sunset mu Nkhalango ya Coronado yaku Arizona? Ndichiyani chinthu ichi chachilendo chimene chinachitika kumtunda kemeneko, chimene anthu akhala akuyenda kuchokera kumadzulo kupita ku m'mawa, kutola miyala imene inali kozungulira nkonseko kumene Icho chinakantha? Ndipo umodzi uliwonse wa iwo, mwala umodzi uliwonse, uli ndi ngodya zitatatu pa iwo, umene Icho chinaswa. (Utatuwo ndi Mmodzi.) Iyo ili pa madesiki, pa zopsyinjira mapepala, ku fuko lonseli. Nchiyani chinthu chachilendo ichi pa phiri la Sunset mu Nkhalango ya Coronado?

70 Junior Jackson akumvetsera kuno, inu mukukumbukira loto limene iye anali nalo limene ine ndinatanthauzira, "Ndikupita cha kolowera kwa dzuwa?" Ndipo izi zinachitika pa phiri la "Sunset." Ndi

nthawi ya madzulo, nthawi ya kulowa kwa dzuwa. Uthenga wakulowa kwa dzuwa kupyolera mu kutha kwa mbiri ya kale, kutha kwa uneneri, kani, kukhala zikukwaniritsidwa. Ndipo kudzakhala kuli kuwala pa nthawi ya madzulo, pa Phiri la Sunset mu Nkhalango ya Colorado, mailosi makumi anai ku mpoto kwa Tucson. Kafikeni pa mapu ndipo mukaone ngati Nsonga ya Sunset apo. Ndi ndendende kumene izi zinachitikira. Ine sindinali kuzidziwa konse izo mpaka tsiku lina.

71 Chirichonse, chimene... Icho sichidzafa konse. Icho chingodzifunyulula chokha mopitiriza. Kuchokera ku chinthu chomwecho chikuchitika, mpaka kuchithunzi cha kukhala Yesu atayima akuyang'ana pa ife; ndipo tsopano ndendende pa phiri la Sunset, ndi kuwala kwa kulowa kwa dzuwa. Kuwala kwamadzulo kwafika, Mulungu akutsimikizira Yekha. Nchiyani ichi? Ndi zoonza kuti Mulungu ndi Khristu ali mmodzi. Yoyera...Ndi angati analiwona ilo, wigi yoyera pa Iye, monga ife tinayankhula mu Chivumburutso 1? Mwaona, Umulungu wapamwamba, ulamuliro wapamwamba; palibe liwu lina, palibe Mulungu wina, palibe chinthu china! "Mwa Iye muli chidzalo cha uMulungu m'nthupi." Angelo iwo omwe anali wigi Yake. Amen.

72 Nchiyani chinachitika pa phiri la Sunset? Mulungu kutsimikizira Mawu Ake. Ichi ndicho chomwe phokoso lonse liri. Zindikirani, ndi Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake olonjezedwa kachiwiri, aChivumburutso 10:1 mpaka 7, "Ndipo mumasiku akuomba kwa Uthenga wa Ngelo wachisanu ndi chiwiri, chinsinsi cha Mulungu chiyenera kuti chitsirizidwe." Chinsinsi chobisika cha Chivumburutso 10:1 mpaka 7, Uthenga wotsiriza kwa m'badwo wotsiriza. Zikukwaniritsa ndendende, mu m'badwo uno, Luka woyera 17:30, "Tsiku limene mwana wa mnthu ati adzaulidwe."

"Ndipo kudzauka aneneri onyenga ndi aKhristu onyenga kusonyeza zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa mochuluka kuti zikanati ziwanyenge osankhidwa ngati nkotheke." Anthu adakali mukukaika. Ndipo, mwachizolowezi, mpingo naonso ndiwodabwitsika basi.

73 Ndipo sayansi, konse ku Tucson yense panobe iwo akulemba zidutswa ndikuziika mupepala. Kumbuyo komwe uko pa phiri la Lemmon, makamera akulu awo sanachiwone icho akukwera m'mwamba kuchokera pamene ife tinali titaima. Kutsetsererika cha kumadzulo, kusonyeza kuti nthawi yatha. Izo zizingakhoze kupita koma chidutswa chaching'ono m'menemo; ziri ku Gombe la kumadzulo. Chiweruzo chinangokantha mwanjira imene icho chinapitira. Kupita kumene m'mwamba pa Phoenix ndi modutsa kumene, mpaka ku Prescott ndi kudutsa mapiri mpaka kuchigwa chakumadzulo, kupitirirabe mpaka.... Kodi iwo anali akupita kuti? Kukwera pamene mpaka mu Alaska, ndipo Iye akubingula, kulunjika njira imeneyo.

74 Ndipo zoyang'ana m'mwamba ndiwonse aiwo mu Tucson akadafunsabe, ofufuza za Sayansi akuyesa kuti apeze icho chiri. Pamwamba kwambiri mwakuti sikungakhoze kukhala chifunga, nthunzi, kapena kanthu kena m'mwamba umo. "Nchiani chinachita izo? Kodi zirikuti izo?" Iwo angokhala odabwitsidwa ndikuwala kwa uzimu uko kutapachikika patali mumulengalenga monga iwo anali pamene Amagi ankabwera akutsatira nyenyezi, akuti, "Alikuti Iye yemwe wabadwa ali mfumu ya Ayuda?" Chinali chiyani icho? Mulungu kukwaniritsa Mawu Ake, "Ndipo kudzatuluka nyenyezi kuchokera kwa Yakobo."

75 Ndipo Mulungu wakumwamba analonjeza kuti nthawi yamadzulo ikanati idzakhale ndi kuwala kwa madzulo. Zaka zitatu zapitazo chinsinsi ichi chinali uneneri, "Ndi nthawi yanji ino, bwana?" koma tsopano ndi mbiri yakale. Izo zadutsa. Lonjezo lakwaniritsidwa. Ndi nthawi yanji ino, bwana, ndipo nchiyani chokopa ichi? Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

Tiyeni tipemphere.

76 Wokonedwa Mulungu, Ine ndawasunga anthu awa kwanthawi yayitali, motalika kwambiri kuposa momwe ine ndinalinga. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti china chake chikananenedwa kapena kuchitidwa chimene chiti chiwapangitse anthu kunja kulikonse kuti amvetse. Ndipo pakuona ndikumvetsa iwo akhoze kukhulupirira kuti inu ndi Khristu wowona, ndipo Mawu amene akukhala akutsimikiziridwa ndi kutsimikizira kwa Mawu Ake kukhala angwiro ndikukhala akukwaniritsidwa mu nyengo yake.

Tsopano, Ambuye Yesu, kuchokera mu Mawu Anu Omwe, inu munanena kuti dziko lidzakhala muchikhalidwe cha Sodomu. Ife tikudziwa izo, ife tikukhoza kuyang'ana pa izo. Ndipo inu munati, mutsiku limenelo, "Monga zinali mu Sodomu." Uku kunali amithenga atatu anatumidwa ku dziko la Amitundu ndi Ahebri. Ndipo m'modzi wa iwo, yemwe anali Mulungu mwini wake, Mwana wa munthu anadziulula yekha mumawonekedwe a umunthu ndipo anachita chozizwitsa, mochuluka kuti anamuuza Abrahamu zimene Sarah anali akuchita kuseli kwa Iye mu hema.

Inu munati izo zikanati zidzabwereze kachiwiri pamene dziko lonse la amitundu likanati lidzakhale muchikhalidwe cha Sodomu. Ndipo ife tiripano, Ambuye. Ma uneneri ena akutsimikizira chinthu chomwecho, za kutumiza Eliya mumasiku otsiriza, mzimu wa Eliya pa dziko lapansi, kuti abweretse mitima ya makolo, kapena, "Ana kubwerera kwa makolo." Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti ora lino kuti Inu muwatsimikizire Mawu Anu, kuti inu muli yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Perekani izo, Atate. Iwo wonse ndi Anu. Ine ndikupemphera kuti inu mupereka madalitso awa ndikutsimikizira zimene zanenedwa, kwa Ulemerero wa Mulungu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

77 Kuti uyankhule mawu, ndi munthu; kutsimikizira mawu, ndi Mulungu. Kuti unene chinachake, ndichinthu chimodzi; Mulungu kuti achichite icho ndi chinthu china. Mulungu samasowa otanthauzira aliyense; Iye amachita kutanthauzira kwakekwake.

Tsopano ife tikukonzekera kuti tikhale ndi mzere wa pemphero, kuti tipempherere odwala, Mulungu akalola. Ndipo ife tikudziwa kuti palibe m'modzi, palibe mwamuna, palibe mkazi, palibe munthu wokhalapo, palibe M'ngelo, yemwe angakhoze kukuchizani inu, pakuti Mulungu anachita kale izo. Iye anapanga kukonzekera chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita ndikuzirandira izo.

78 Palibe munthu, palibe M'ngelo, palibe chinthu, osati ngakhale Mulungu Mwiniwake, angakhoze kukukhulukirani inu pamachimo anu. Izo zonse zinachitidwa kale. Yesu anachita izo pamtanda. Koma izo sizidzakuthandizani konse inu, kapena chirichonse, kukupindulirani inu chirichonse, mpaka inu mutazivomereza izo, Mukuona.

Chinthu chokha chimene chingakhoze kuchitidwa, ndi zolamula zomwe zaperekedwa ndi Mulungu, kwa okhulupirira kuti adziika manja kwa odwala. Izo zakhala ziri kupyola mumibadwo iwo achita zimenezo, kupyolera muzitsitsimutso. Ndipo iwo azitcha izo, Mulungu.

79 Abrahamu anaona zizindikiro zochulukira. Koma inadza nthawi pamene Abrahamu anawona chizindikiro chake chotsiriza, Sodomu asanati awotchedwe kumene, ndipo izo anali Mulungu akuziwonetsera Iye yekha mwa mawonekedwe a munthu. Kodi inu mukukhulupirira izo? Kodi Yesu anati izo zikanati zidzabwerezenso?

80 Tsopano, ndi angati mkati muno... Ndi kunja muwayilesi... kapena kunja pa lamya kudutsa fukoli, ngati inu mukummvetserabe kuno, konzekerani tsopano kupemphero, khalani mukupemphera, ndipo inu amene muli ndi mipango... Tsopano, ine sindingakhoze kumuuzza Mulungu choti achite. Ayi, izo zikhale kutali ndi ine ngakhale kuyesera izo. Iye ndiwochita mwayekha; Iye amachita zimene Iye akufuna kuchita. Ine ndikhoza kungovomera ndikungokhoza kunena zimene Iye anena.

81 Ndipo Tsopano iwo aimirira kuzungulira makoma, iwo adzazana mkati, athinana. Ine ndikudabwa ngati ife tikanakhoza kumufunsa Mulungu pa Mawu awa, "Ndichiyani chokopa ichi?" Ngati Mulungu akanati ayende pakati pathu kachiwiri (pakhoza mwina kukhala alendo pano), ndikuyenda pakati pathu ndi kusonyeza nkhope Yake yodala pakati pathu, kusonyeza Mzimu Wakeake pano, kusonyeza kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndikwanthawi zonse, kuti aliyense waife (atatha maUthenga awiri amphamvu awa) akanakhoza kukhulupirira izo kuti ziri chomwecho? Kodi inu mungakhoze kuchita izo? Chabwino.

82 M'malo mwa kuitana mzere wa pemphero, ndiye; kwatentha, tadzadzana, kuima motsamira khoma. Ine ndikuyang'ana mbali iyi kuti ndiitane mzere wanga wa pemphero, iwe sungakhoze kuchita izo; kuona, ataima apo. Kodi ine ndikanati ndiitane iwo mbali iyi? Odwala anu, machira, chinthu chirichonse, atagona; sungakhoze kuchita izo. Chotero khalani pamene inu mulipo, ndipo mukhulupirire Mulungu. Ngati inu muli nalo khadi la pemphero, ligwireni ilo, zikhala ziri bwino. Ife tifika kwa inu ngati inu mukufuna kuti mubwere kudzera mumzere. Koma inu simukusowa kubwera kudzera mumzere.

83 Bambo Shepherd aja, la mulungu latha usiku, sanabwere konse kudzera mu mzere ine sindiri - ine sindiri kulingalira kuti iye anali ndi khadi la pemphero. Kodi bambo Shepherd alimuno usiku uno? Kodi ali pati iwo? Kodi iwo alimuno? Iwo ali kumbuyo. Kodi inu munali ndi khadi la pemphero, bambo shepherd? Inu munalibe? Iwo analibe. Iwo akhala kumbuyo komweko kachiwiri, usiku uno. Ndiwo malo abwino kukhalapo, M'bale Shepherd.

84 Osati kokha kuti muyenera kukhala pamenepo, koma ingokhalani ndi chikhulupiri. Pakuti, kumbukirani, mkazi wang'ono anakhudza chovala chake ndipo iye anamverera izo. Ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawi zonse. Ndipo kalata ya Aheberi, muchipangano chatsopano, ananena kuti Iye ndi wansembe wankulu usiku uno yemwe akhoza "Kukhudzidwa ndikumverera kwa zifooko zanu." Kodi inu mukukhulupirira izo? Khalani nacho chikhulupiri ndiye! Musati mukayike izo. Khulupirani izo, ndipo izo zifika pochitika. Inu mukhoza kukhala nazo zimene inu - zimene inu mwazipempha ngati inu mungakhoze kukhulupirira izo. Koma inu muyenera kuti mukhulupirire izo. Kodi inu muchita izo? Kodi nonse inu mukhulupirira izo? Ndi angati ati akhulupirire izo tsopano? Mulungu akudalitseni.

Ine sindikudziwa uyu ndani ndi uyu ndani. Ine sindikudziwa aliyense wa inu. Iyo sintchito yanga kuti ndikudziweni aliyense wainu. Iyo ndi ntchito ya Mulungu kuti adzidziwa zinthu izi. Koma Iye achita izo ngati inu muti mukhulupirire izo. Kodi inu mukukhulupirira izo tsopano?

85 Tsopano, wokonedwa Mulungu, zedi ife sindife gulu la aKhristu a haibridi - ife sitiyounera kukhala tiri - wina wake yemwe ayenera kuti adzisasatizidwa ndi kuleledwa. Inu mulibe amtundu umenewu, Ambuye. Inu mulinawo okhulupirira opirira. Kukhalapo kumene kwa Mulungu kumyatsa mtima wa munthu pa moto. Monga Abrahamu, iye anakhulupirira Mulungu. Inu munadzipangitsa nokha kudziwika kwa iye, ndiye inu munawonekera kwa iye ndipo munachita chizindikiro, ndipo iye anakukhulupirirani Inu. Inu munatembenuza thupi lake kubwerera ku unyamata, ndiponso mkazi wake, chimene, mkazi wake anali

gawo la thupi lake lomwe. Ndiye kunabwera mwana watsopano, mwana olonjzedwa.

86 Mulungu, inu munalonjeza kuti izo zidzakhala zinthu zomwezo mutsiku lino. Ine ndikupemphera kuti inu mutsimikizire Mawu awa. Ndipo ife tichita palonjezo limodzi lomwelo ilo apo, kuti izo zikhale monga izo zinani muSodomu, Sodomu asanati awotchedwe kumene ndipo chiweruzo chinakantha Sodomu, dziko la amitundu. Chotero chiweruzo chiri kukonzekera kuti chikanthe dziko la amitundu, ndipo aYuda alinazo zaka zina zitatu ndi theka kuti adutse nthawi ya chisautso, vuto la Yakobo, kupitiriza kwa masabata asanu ndi awiri ADanieli. Koma, amitundu awerengedwa, ndi nthawi ya kupita. Ndipo inu munapereka chizindikiro chimenecho, ndipo inu munati icho chikanati chidzakhalenso. Perekani izo, Mulungu. Iwo ali, ife tiri mumanja anu, chitani ndi ife monga inu mukuona zoyenera. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

87 Tsopano musati mukhale amanjenje. Zikanati zikhale zotani ngati ine ndikanakhala wa manjenje? Tsopano, ine ndikupanga chinthu pano chimene chiyenera kudalira pakuchita mwayekha kwa Mulungu. Koma nchifukwa chiani ine ndikuchita izi? Iye anati izo zikanadzakhala. Izo zikukhazikitsa icho. Ndipo ngati iye akudzipanga yekha chimenecho, kutsimikizira monga choncho pamaso panu, chabwino, kodi inu simungakhoze kumukhulupirira Iye? Ndithudi. Inu mungakhala nacho chikhulupiriro tsopano ndikukhulupirira.

Ndiloreni ine ndingoyang'ana pozungulira, ndiwone kumene Mzimu Woyera uti unditsogolere, chimene Iye atachite. Ine sindikudziwa chimene Iye atachite, izo ziri kwa Iye. Koma ngati inu muti mungokhala nacho chikhulupiriro, kungomukhulupirira, "Zinthu zonse nzotheke kwa iye amene akhulupirira." Kodi nonse ainu mukukhulupirira izo, kwezani mwamba manja anu ndikuti, "Ine ndikukhulupirira izo." (Osonkhana, anena "Ine ndikukhulupirira izo." - Mkozi.) Ndi mtima wanga wonse ine ndikukhulupirira izo.

88 Tsopano katatu kakhala kutsimikizira, ngati Iye ati achitye izo nthawi zitatu zolunjika kuti akutsimikizireni inu kuti izo ndi zolondola. Ine sindikusamala kumene inu muli, yemwe inu muli, inu mungokhala nacho chikhulupiriro ndipo mukhulupirire. Tsopano, musati mugwedezeke apo. Mbali iyi.

Dona, akupemphera, ine sindikukudziwani inu. Inu mungokhala pamene muli; inu simukusowa kuti mubwere ine sindikukudziwani inu, koma inu mwagwiriziramsungwana wam'ng'ono m'dzanja lanu, kapena pamiyendo panu. Ndine mlendo kwathunthu kwainu. Ndipo msungwana wam'ng'onoyo akuwoneka wabwinobwino, iye akuwoneka bwino. Iye ndi msungwana wam'ng'ono wokongola, msungwana wam'ng'ono wa mutu - wofiira. Ine ndikumuyang'ana pano, iye sakuwoneka ngati ndi wolumala kapena chirichonse. Ine sindikudziwa chimene chiri vuto ndi iye. Zikhoza kusakhala zamwanayo; zikhoza kukhala zainu. Koma ine ndinangopezeka ndikukuonani inu mutakhala apo muli ndi mwana ameneyo, ndipo mukupemphera. Ine ndinayenera kuyankhula ndi inu kwa mphindi, kuti ndiugwire mzimu wanu, monga Yesu ananena kwa mkazi, "Ndibweretsere ine akumwa," mwaona, kungoti ndidziwe - ndidziwe zamunthu m'modzi. M'bale Bryant ndi awa akhala panowa, ine ndikuwadziwa anthu awa amene akhala panowa iwo akhoza kukhala osowa nawonso, koma inu, munali mulendo.

Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? Kodi inu mukukhulupirira zinthu izi zimene inu mwazimva usiku uno ndi Choonadi? Tsopano, ngati Mulungu ati awulule kwa ine china chake chomwe inu mwachita, kpena china chake chomwe inu simumayenera kuchichita, kapena china chake chiri cholakwika ndi inu, kapena chimene chokhumba chanu chiri, inu mudziwa ngati icho chiri choona kapena ayi. Simutero inu? Ndipo ngati Iye atachite izo, kodi izo zitsimikizira Mawu Ake kuti Iye aliyemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse, ndipo ndikuti Luka woyera 17:30 akukhala akuwonetseredwa? Inu mukukhulupirira izo?

89 Tsopano, dona anadzutsa dzanja lake kuti ndife alendo. Ine sindikukudziwani inu, koma ine ndikuyesera kuwukhudza mzimu wake, munthu m'modzi. Mulipo wochuluka a inu amene mukukoka. Tsopano, inu mukhulupirire ichi ndi mtima wanu wonse. Tsopano, izo ndi zammsungwana wang'ono wasati inu. Ndinu wa manjenje, koma simanjenje amene akukuvutitsani inu. Chinthu chachikulu pa mtima wanu ndi mmsungwana wam'ng'ono uyo. Ndipo inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine chimene icho chiri? Inu mukukhulupirira izo? Kodi icho chingakuthandizeni inu, kodi inu mukanati mukhulupirire ndiye? Ndikuvulala kwa ubongo. Ndikulondola uko? Tsopano ikani dzanja lanu pa mutu wa mwana wang'onoyo; dzanja lanu.

90 Wokonedwa Mulungu, inu munati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Iwo adzaika manja awo pa odwala ndipo iwo adzachira." Mkaziyo ndi wokhulupirira. Dzanja lake liri pa mwana. Mulore iye achire. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupereka pemphero iri. Amen.

Tsopano kodi inu mukukhulupirira, nonse inu? Ngati inu mungakhoze kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheke. Ndithudi!

Ine ndikumudziwa dona yemwe wakhala pafupi ndi iye, koma iye akuyang'ana modzipereka kwambiri mbali ino. Ine sindingakhoze kumutchula dzina lake, koma ine.... Ngati ine ndiyang'ana pa iyemphindi, ine ndidziwa. Koma ndimudziwa mkaziyo maonekedwe, koma ine sindikudziwa limene liri vuto lanu. Kodi inu mukundikhulupirira ine.... Mulungu andirora ine kudziwa limene vuto lanu? Kodi inu.... Kodi izo

zingakuthandizeni inu? Matenda a shuga. Tsopano, ngati uko ndi kulondola, kwezani dzanja lanu. Ndithudi!

Zinapezeka kuti ndi dona wagona.... Wakhala pafupi ndi inu, ali ndi chinthu chomwecho. Iye ndi mlendo. Dona winayo akupempherera wina wake, mwana olumala. Inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, Mulungu angakhoze kupereka izo.

91 Wina wake mbuyo mkati umu. Mwamuna wakhala cha uko, akuyesera kuti asiye kusuta ndudu. Inu mukukhulupirira Mulungu achotsa izo kwa inu? Chabwino. Inu mukukhulupirira? Inu mukhoza kukhala nazo izo? Ine sindinamuonepo konse bamboyo m'moyo wanga.

Pano pali mwamuna. Mukuwona nthunzi wa mdima uwo wapachikika pamwamba pa mwamuna uyu apa pomwe yemwe wagona kukhala ngati pa machira, kapena mpando? Iye akufa. Iye ali ndi nthunzi. Iye ali ndi khansala. Ine sindikumudziwa bamboyo, sindinamuwonepo konse iye. Mulungu akudziwa zonse za inu. Ndicho choonadi bwana. Inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine china chake chokhudza inu? Kodi icho chikanati chikuthandizeni inu kuti mulandire machiritso anu? (m'bale ati, "inde ine nditero." - Mkonzi.) Inu munabweretsedwa kuno ndi nzanu. Koma sindinu ochokera kuno, ndinu akwina kwake kumene kuli malo akulu amadzi m'mene anthu amawedzako. ("Eya") eya, Albany, Kentucky. ("Ndiko kulondola") ndiko kulondola. Khulupirirani. Ndipo inu mukhoza kubwerera kwanu, wabwino. Khulupirirani kuti izo zachoka. Ngati inu muti mukhulupirire izo! Inu muyenera kukhulupirira izo, ndipo mukhulupirire izo zachitidwa kwa inu. Inu mukukhulupirira?

92 Inu, ochokera ku Tennessee, muli ndi mnyamata ali ndi mphumu. Osati kuno koma inu mukukhulupirira kuti iye achiritsidwa? Ndiye tengerani mpango wanu, wanu.... Uli mdzanja lanu pamenepo kwa iye. Iye achiritsidwa ngati inu muti mukhulupirire izo.

Dona akulira, yemwe wakhala mbali ina kwa doctor Vayle apo. Iye ali ophimbidwa, nayenso, nthunzi wakuda. Ine sindinamuonepo mkaziyu mu moyo wanga, koma iye ali ndi khansala. Iye afa ngati chinachake sichichitika pa iye. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akuchiritsani inu, dona? Inu mukhoza? Kukhala nawo machiritso anu, ngati inu mungokhulupirira.

Pali dona wang'ono yemwe wakhala kumbuyo kwake komweko ali ndi mpango pakamwa yake. Iyenso ali ndi m'mimba mwa nsungu, akudwala. Inu mwakhala muli nazo nthawi za kukomoka, kupangitsa khungu, kugwera pena. Wina wake wakubweretsani inu kuno. Inu muli ndi vuto la ukazi. Ngati inu muti mukhulupirire, inu mukhoza kupita kunyumba, kukakhala bwino.

93 Iwe, mnyamata, ndiwe mlendo; wakhala apa pomwe patsogolo paine, ukuyang'ana pa ine. Kodi ndiwe chiani, wakuPuerto Rico kapena china chake? Eya, chimene ine ndikutanthauza....?....! Ndine mulendo kwa inu. Inu mukudziwa izo; sindinu ngakhale wochokera mu dziko langa. Koma inu mukukhulupirira kuti mulungu akhoza kukupatsani inu chokhumba cha mtima wanu? Ngati ine nditakuuzani inu chimene chiri chokhumba chanu, kodi inu muzilandira izo? Inu mukufuna ubatizo wa Mzimu Woyera. Izo ndi zoono. Landirani Mzimu Woyera, m'bale wanga.

Pano pali bambo wachikuda wakhala kumbuyo komwe uko, ali ndikulemedwa pa mtima wake. Ndi kwa mkazi wake. Iyeyo sali kuno, ngakhale. Iye ali ndi vuto ndi mapazi ake. Inu mukukhulupirira kuti Iye amuchiza iye? Inu mukutero? Ndinu mulendo pano. Ndinu wochokera kutsidya kwa Nyanja. Ndinu wochokera ku Jamaica. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Bambo Brady. Inu mukukhulupirira? Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawi zonse.

94 Dona uyu wakhala pambuyo pomwe chapamapeto awa pafupi ndi akazi a Wright apo, iye ali ndi kulemedwa pa mtima wake. Iye akupempherera mwana wake wa mkazi. Iye wabwera kudzachitidwa oparesoni. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, chifukwa cha iye? Iye sasowa izo ngati inu muti mumufikitse kokha iye kuti akhulupirire izo. Ine sindingakhoze kuchiza.

Kumbuyo uko patali molerera ana, ine ndikuona Mzimu wa Ambuye, M'ngelo, kuwala kukusunthila molerera ana. Iwo uli pa mkazi wam'ng'ono ndipo iye ali ndi vuto la uzimu lomwe iye akulidabwa. Zikuoneka ngati ine ndiyenera kuti ndizimudziwa mkaziyo, mulimonse, mkazi wam'ng'ono. Iye nayenso ali ndi kusokonezeka kwa ukazi. Inde. Dzina lake ndi akazi a West, ochokera ku Alabama, akazi a Davide West. Khulupirirani; Mulungu apereka izo kwa inu.

95 "Kudzakhala kuwala, ndipo mutsiku limenelo pamene Mwana wa munthu akhala akuwululidwa." Ngati Iye Sali Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse, ine sindikudziwa kanthu kaizo. Kodi inu mukukhulupirira izo? Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo akukhulupirira.

Kunja pa zoyankhulirapo kudutsa dziko tsopano, ndimukachisi uyu, ndi angati ainu muti mukweze manja anu ndikuti, "ine ndine wokhulupirira?" Tsopano, inu kunjani uko mumaiko, aliyense amene wakweza m'mwamba dzanja lake pano. Ndikutali kunjani kutsidya kwina kwake kudutsa mafuko, inu mwakweza m'mwamba manja anu, mopanda kukaika. Tsopano tsekani maso anu, ingogwetserani manja anu kwa wina wapafupi ndi inu gwirani dzanja lawo. Likeni ilo pa phewa ine ndaika manja anga pa mipango.

Taonani zimene zachitidwa lero! Taonani zimene zachitidwa tsopano.

Kuona nkhope yake yolemekezeka

Yowala ndi chikondi cha umulungu!

Odala olandira zachisomo chake,

Monga ngale mu korona wake kuti tidziwala.

Tsopano dzipempherani. Tiyeni tipemphere, kulikonse.

96 Wokonedwa Mulungu, ora lafika. Izi zikutanthauza chiani? Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake! Nchiyani chokopa, Ambuye? Ndi Mulungu akukwaniritsa Mawu Ake ndi chiyani ichi uko kudutsa fuko, kudzera munjira ya lanya, kuti mazana a anthu ali ndi manja atayikidwa pa wina ndi mzake mufuko lonse, kuchokera ku Gombe limodzi mpaka kwina, kuchokera kumpoto mpaka ku m'mwera, kum'mawa mpaka kumadzulo? Pano pakhala anthu ochokera kumaiko akunja, maiko ochuluka, Mexico, Canada, ndipo ife tiri ndi manja athu atayikidwa pa wina ndi mzake. Mulungu akuwakwaniritsa Mawu Ake!

Izi ziri motani kuti munthu akhoza kuyima pano mwa Mzimu Woyera ndi kumuitana munthu monga Iye anachitira Simoni Petro, "Dzina lako Simoni, iwe ndi mwana wa Yonasi?"

"Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno."

"Ine ndiribe mwamuna."

"Zoonadi. Iwe uli nawo asanu."

Iye anati, "ine ndikudziwa kuti Mesiya akudza kuti adzachite izi, koma inu ndinu Yani?"

Iye anati, "Ine ndine Iye."

97 Ndipo ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse. Ndipo inu munalonjeza, "Ntchito zimene ine ndikuchita inunso mudzazichita. Zochuluka kuposa izi inu mudzazichita, chifukwa ine ndikupita kwa Atate." "Ndipo wonani, mumasiku otsiriza ine ndidzakutumizirani inu Eliya, mneneri, ndipo iye adzasintha malingaliro a anthu, kutembenezira mitima ya ana kubwerera ku chiphunzitso cha Apostoli cha m'Baibulo." "Ndipo kudzakhalala kuwala munthawi ya madzulo."

Ife tiri pano, Mulungu wamkulu wakumwamba! Oralo liri pano! Manja ayikidwa pa anthu.

Satana, iwe wagonjetsedwa. Iwe ndiwabodza. Ndipo, ngati wantchito wa Mulungu ndipo ngati antchito, ife tikulamulira chimenecho mu Dzina la Yesu Khristu, kuti iwe umvere Mawu a Mulungu, ndikutuluka mwa anthu, chifukwa kwalembedwa, "Mu dzina langa iwo adzatulutsa ziwanda."

Ndipo anthu onse akhale omasulidwa. Perekani icho, Mulungu okonedwa. Inu ndinu Mulungu wakumwamba amene munagonjetsa, tsiku lija ndi chokopa pa phiri la Kalvare, kudwala konse ndi matenda onse ndi ntchito zonse za mdierekezi. Inu ndinu Mulungu. Ndipo anthu achiritsidwa ndi mikwingwirima yanu. Iwo ndiomasuka. Mudzina la Yesu Khristu. Ameni.

98 Mulungu, mpango uliwonse omwe uli apa, pamene Mzimu wa Mulungu udakali pano, pamene kudzodza kwa Ambuye Yesu Khristu kuli pa anthu awa, ndipo zizindikiro zazikulu zomwe Iye analonjeza zikukwaniritsidwa, ndipo dziko likunjenjemera, zibvomerezi zikuchitika, zizindikiro zazikulu zomwe Iye ananena, ndi Lemba likukwaniritsidwa, ndi kuwala kwa madzulo kukuwala. Ine ndikuyika thupi langa pamwamba pa mipango iyi, kuimirira thupi lonse ili la okhulupirira kuchokera kum'mawa, kumadzulo, kumpoto, ndi kum'mwera; ndipo ndikunena kwa mdierekezi, "Mu dzina la Yesu Khristu musiyeye odwala aliyense yemwe izi zikayikidwe pa iye," Ku ulemu ndi ulemero wa Mawu a Mulungu. Mu dzina la Mawu a Mulungu, Yesu Khristu waku Nazareti. Ameni.

99 Tsopano, mwakachetechete, ndimalingaliro abwino, mwakhalidwe, ndi mumaganizo anu abwino, ngati okhulupirira, kodi inu tsopano mukukhulupirira ndikulandira machiritso anu kuchokera kwa Mulungu Wamphamvu zonse, mu Dzina la Yesu Khristu? Ngati inu mukutero imikani manja anu. Nonse uko osiyanasiyana kumadera, imikani manja anu kunjauko. Munthu aliyense mukati muno, motalikira monga ine ndingaone, anali ndi manja awo m'mwamba; mkati, kunjauko, oima m'mazenera, mudzitseko, moyamwitsira ana, ndi kuzungulira kwina konse, anthu ayimika manja awo. Iwo achilandira icho. Satana wagonjetsedwa! Mikwingwirima ya Yesu Khristu yakuchiritsani inu, ndi kupezekapo kwa Yesu Khristu kukutsimikizira lingaliro loti Iye ali ndi Moyo lero, okhala ndi kuthekera nthawi zonse kusungu malonjezo onse amene Iye anachita. Ameni! Ine ndikumukhulupirira Iye. Inu mukutero? (Osonkhana anena, "Ameni." - Mkonzi.)

100 Tsopano tiyeni ife tiyimirire pa mapazi athu. MuDzina la Ambuye Yesu, kulandira china chirichonse chomwe chachitika kapena kulankhulidwa, ife timamukonda Iye ndi mitima yathu yonse. Timamulemekeza

Iye ndi zonse zomwe ziri mwaife. Ndiyeno pamene inu mukupita m'makwanu mosiyana kuchokera usiku uno, Mulungu apite ndi inu. Mulungu akupatseni inu Mzimu Woyera ngati inu mulibe Mzimu Woyera.

101 Mamuna aliyense, mkazi, mnyamata, kapena msungwana, pano, amene sanabatizidwepo muDzina la Yesu Khristu, apo pali zovala, dziwe. Osaika mawa zomwe zingathe kuchitika lero. Mawa litha kukhala mochedwa. "Zikwanire tsiku, pakuti tsiku liri ndi zobvuta zake." Apa pali azitumiki omwe ayimirira, akudikirira, zobvala zikudikirira. Palibe zowiringula. Kodi inu mukudikirira? Ngati muli, khulupirirani. Ziribe kanthu momwe inu munabazidwira, mokonkhedwa, motsanuliridwa, china chirichonse chomwe chiri, izo ndizolakwika. Kuwala kwafika. Bwerani, khulupirirani, ndipo mubatizidwe.

Aliyense opanda Mzimu Woyera, mulandire Mzimu Woyera, aliyense wainu muchidzalo cha Mphamvu ya Umulungu ndi chikondi zimene Iye analonjeza kwainu, kukupangani inu cholengedwa chatsopano mwa Iye. Ambuye adalitse inu.

102 Tsopano, mpaka laMulungu linalo m'mawa nthawi itangopitirira 9 ndi theka, tiyeni tiyimbe nyimbo yaying'ono iyi imene tinkakonda kuyimba zaka zapitazo.

Musaiwale pemphero la pabanja,
 Yesu akufuna akakumane nanu kumeneko;
 Iye azasamalira zanu zonse,
 Musaiwale pemphero la pabanja
 Tiyeni ife tiyimbe iyo pamodzi tsopano.
 Musaiwale pemphero la pabanja,
 Yesu akufuna akakumane nanu kumeneko;
 Iye azasamalira zanu zonse,
 O, Musaiwale pemphero la pabanja

Tsopano pamene tikuimbanso kachiwiri, gwiranani chanza ndi muyendamnjira yemwe ali pafupi ndi inu, mwaona, pamane ife tikuyimba iyo.

Musaiwale pemphero la pabanja,
 Yesu akufuna akakumane nanu kumeneko;
 Iye azasamalira zanu zonse,
 O, Musaiwale pemphero la pabanja

103 Kodi inu simukumukonda Iye? Ine ndikumukonda Iye. Inde ndikumukonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine ndipo anagula chipulumutso changa (icho chinali chokopa) pa phiri la Kalivare. Ndichokopa chomwecho pa phiri la Sunset, pa phiri la Nebo, pa phiri la Sinayi, zochitika zonse zosiyana zapamwamba pa mapiri. Ndiye, chabwino, tiyeni ife tiyimbe iyo tsopano.

Ine ndikumukonda Iye, Ine ndikumukonda Iye
 Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
 Ndikugu ... Chipulumutso
 Pamtengo wa Kalivare.

Onse amene amamukonda Iye, anene, "Ameni." (Osonkhana anena, "Ameni." - Mkonzi). Zikhale choncho! Tsopano tangolingalirani za chomwe Iye wakuchitirani inu; ganizani, kuti inu munakakhala muli kunja uko mu nyumba yomwera mowa usiku uno. Inu mwina munakakhala muli mumanda monga m'mnene ine ndikanakhallira, kunja kwa zifundo za Mulungu. Kodi Iye anakuchitirani chiyani inu? O, tingathe bwanji ife kukhala osamukonda Iye? Sizipanga kusiyana kwina kulikonse zomwe wina aliyense akunena, Iye ndi oyamba.

104 Tiyeni titseke maso athu, ndikuweramitsa mitu yathu pamene tikuyimba iyo kwa Iye tsopano. Iye amakonda nyimbo, kuyimba nyimbo za mbukhu. Tiyeni tiyimbe iyo kwa Iye tsopano.

Ine ndikumukonda Iye, Ine ndikumukonda Iye
 Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
 Ndikugula Chipulumutso changa

Pamtengo wa Kalivare.

Ndi mitu yathu komanso ndi mitima yathu yoweramitsa mukupezekapo Kwake, ndi mayamiko pazomwe maso athu awona, zomwe makutu athu amva, zomwe zalembedwa mu Mawu a Mulungu, chomwe lonjezано lake lakhala kwa ife lero. Mulungu akudalitseni.

105 Ife tiri ndi - ndi mlendo usiku uno, M'bale Ned Everson, yemwe anali mtumiki ku mpingo wa Presibeteria. Atate ake, azibale ake, ndi azitumiki ku mpingo wa Presibeteria. Iye, ine ndamvetsedwa, wabatizidwa lero, kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu. Iye ndi Mtumiki, ndipo wabwino pa chimenecho. Ndipo tsopano ine ndikufuna kumupempha Iye, monga ine ndikukhulupirira kuti ndi wantchito wa Mulungu kuti, apemphe madalitso a Mulungu pa osonkhana awa, pamene inu mukupita kwanu.

M'bale Everson bwerani patsogolo pano, pamene ife taweramitsa mitu yathu ku pemphero. Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga.



www.messagehub.info

Maulaliki wolalikidawa ndi

William Marrion Branham

"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7